

Zisudzo

Chisudzo ndi nkhani yochitika kapena yopeka yomwe imafotokoza zinthu mokhala ngati zikuchitika kumene. Chisudzo ndi chiyerekezo cha zinthu zochitika m'moyo weniweni. Zinthu zotsatirazi zikhudzana ndi chisudzo:

- Chimayerekeza makhalidwe, mayankhulidwe kapena machitidwe a ena
- Chimachitidwa ndi amtengambali m'malo osiyanasiyana monga m'mabwalo, pamisonkhano, pawayilesi ndi wayilesi yakanema.
- Chimakhala ndi phunziro.
- Chimakamba za zinthu zopeka kapena zochitika.

Kufunika kwa zisudzo

1) Kudziwitsa: mwachitsanzo, mabungwe amachita zisudzo akafuna kuphunzitsa anthu zinthu zosiyanasiyana zomwe zogwa kapena zikuchitika m'dziko monga izi: mliri wamatenda, ulimi wamakono, kufunika kosamalira zinthuza chilengedwe, uchembere wabwino ndi ngozi zachilengedwe.

2) Kuphunzitsa: kuchita zinthu zazikulu kuti dziko litukuke monga: kulimbikitsa ufulu ndimtendere, ndale zololerana, chipembedzo, maphunziro abwino, mliriwamatenda, ulimi wamakono, kufunika kosamalira zinthu chilengedwe, uchembere wabwino ndi ngozi zachilengedwe.

3) Kudzudzula: kudzudzula makhalidwe oyipa monga nkhanza, katangale ndi ziphuphu, uchifwamba, kuzemba kulipira msonkho, kupondereza amyeni ndi anaamasiye, chinyengo pamalonda, ulamuliro woipa, miyambo yoipa ndikulemba ana ntchito

4) Kuchenjeza: kuchenjeza za chilango chomwe chingadze akachita zoipa mongakuonera/kubera mayeso, kuononga katundu waboma, kusokonezachisankho cha atsogoleri adziko ndi zina

5) Kusangalatsa: Zisudzo zimasangalatsa anthu kuti aziseka popeza kuseka ndi mankhwalaamphamvu. Munthu wansangala amakhala wamtendere. Ngakhale zisudzo zotere zimachitidwa pofuna kutaya nthawi, zimakhala ndi maphunziro.

6) Kuyamikira: Anthu ena amachita zisudzo zofotokoza mbiri ya anthu omweadachitapo zinthu zazikulu zothandiza dziko kuti litukuke mongakulimbikitsa ufulu ndi mtendere, ndale zololerana, ufulu wachimbedzo, ulimi wothirira, ulimi wamtayakhasu ndi maphunziro abwino.

Magwero

- Mbiri yakale
- Ndale
- Ulamuliro wosiyanasiyana
- Miyambo ndi chikhalidwe

- Udindo

Kayankhulidwe

- Kachibadwidwe(kukweza/kutsitsa mawu)
- Kudziyankhulira
- Kukambirana ndi ena
- Kuyankhula m'zining'a,mikuluwiko ndi mizimbayitso

Kakonzedwe (Zoganizira)

- Zipangizo (zovala),
- Nthawi/nyengo,
- Ochita sewero
- Malo
- Owonera sewerolo

Kufanana kwa zisudzo ndi nkhani zamchezo ndi zolembedwa

- Zonse zimakamba za nkhani zochitika kapena zopeka.
- Mfundo zazikulu zambiri zimafanana.

Kusiyana kwa zisudzo ndi nkhani zamchezo ndi zolembedwa

- Nkhani yachisudzo imalembedwa m'njira yoonetsa kuti zinthu zikuchitidwa ngakhale kuti zina sizichitidwa.
- Mzisudzo mumakhala kukambirana pakati pa amtengambali omwe amachita zinthu mokhala ngati zikuchitikadi.

Kuzukuta chisudzo

1. Mtengambali

Munthu kapena chinthu chomwe chimachita kapena kuchitidwa zinthu mu chisudzo. Pozukuta mtengambali tifotokoze ngati mtengambaliyo ndi wamkulu kapena wamng'ono. Tiyeneranso kufotokoza momveka bwino za makhalidwe a mtengambaliyo mu chisudzomo.

2. Malo ndi nthawi

Komwe chisudzo chikuchitikira komanso nyengo yomwe chisudzo chikuchitikira.

3. Mfundo yayikulu

Zisudzo zimakhala ndi mfundo zazikulu zogwirizana ndi chikhalidwe. Mfundozo ndi monga izi: chikondi, tsoka,kudalirana, kudziteteza, umunthu, chikondi, ulamuliro, zikhulupiriro ndi miyambo.

4. Tsatanetsatane wa nkhani (plot)

Ili ndi dongosolo lamomwe chisudzo chinachitikira. Zisudzo zina zimakhala ndi dongosolo lokhazikika lomwe limakhala ndi magawo aakulu awa:

a. Chiyambi (introduction/exposition)

Ili ndi gawo la chisudzo makamaka koyambirira kwa chisudzo komwe amtengambali, gwero la nthano komanso malo ndi nthawi zimagotokozedwa mwachidule.

b. Chikweza (rising action)

Gawo lachisudzo lomwe limakhala ndi kuyamba kwa chisokonezo (mpungwepungwe) cha m'nthano kaamba ka kulimbana komwe kwachitika.

c. Pampondachimera (climax)

Pamene chisokonezo chafika pachimake m'chisudzo mwakuti kudutsa nthawi imeneyi, chisokonezo chimayamba kuzilala.

d. Mtsetse (falling action)

Ili ndi gawo lomwe limaonetsa kuyamba kuzirala kwa chisokonezo. Gawoli limalunjika ku mathero a chisudzo.

e. Mathero a nkhani (resolution)

Gawo lomwe ndi mapeto a chisudzo

f. Chiyankhulo ndi nsetso (style)

Nsinjiro zachiyankhulo ndi mawu apadera omwe wopeka chisudzo adagwiritsa ntchito komanso zipangizo monga chikumbumtima, mpeputso, mafunso achodziwadziwa, chifanifani, chizindikiritso, voko, chithunzithunzi, mchepso ndi zina zamgulu limeneli.

Zina zoyenera kudziwa m'chisudzo

a. Gawo la chisudzo (act)

Gawo lalikulu la chisudzo (sewero) losonyeza zimene zikuchitika pamalo ena ake.

b. Mtengambali (actor)

Munthu yemwe akuchita nawo sewero (chisudzo)

c. Mpangankhani wotsutsa (antagonist)

Mpangankhani/mtengambali yemwe akunyenga, kusokoneza kapena kuchita zinthu zolimbana ndi mpangankhani wamkulu

d. Mpangankhani wamkulu (protagonist)

Munthu kapena chinthu chomwe chaposa zina kapena mpangankhani yemwe yemwe ali pa phata pa sewero. Pofuna kukwaniritsa cholinga chake, mpangankhani wamkuluyu amapingidwa ndi zinthu kawirikawiri, mpangankhani wotsutsa

e. Zochitika (action)

Zochitika mu nkhani yopeka yomwe imachitikadi kapena imakhala zokamba munthano yaitali, nkhani, ndakatulo ngakhalenso chisudzo (sewero) makamaka powunikira zomwe atengambali/ampangankhani akuchita mu nkhaniyo.

f. Gwero ndi zotsatira (cause and effect)

Mawuwa amayimira ganizo lonena za chiyambi pamene zochita kapena zochitika zimayambitsa zinzake.

g. Maonetsedwe a mpangankhani (characterisation)

Njira zomwe alembic amawumbira ndi kuonetsera ampangankhani awo. Njirayi imatha kuonetsa maonekedwe, zochita komanso mayankhulidwe ndi maganizo a mpangankhani.

h. Chisokonezo(conflict)

Kusamvana kapena mkangano wa mbali ziwiri zosiyana maganizo. Pali mitundu inayi ya chisokonezo:

- cha pakati pa anthu (pakati pa ampangankhani)
- cha iwe mwini (maganizo otsutsana a mpangankhani)
- cha pakati pa munthu ndi gulu la anthu (kusamvana pakati pa mpangankhani ndi anthu, malamulo, miyambo kapenanso sukulu)
- cha pakati pa munthu ndi chilengedwe (mkangano wa mpangankhani ndi zinthu zina zachilengedwe)

i. Kulimbana (Complication)

Zochitika munkhani zomwe zimachititsa mpangankhani wamkulu kuti akhale pachisokonezo

j. Ochita chisudzo (dramatis personae)

Mndandanda wa ampangankhani omwe apezeka m'sewero ndipo kawirikawiri umapezeka kumayambiriro kwa sewero lolembedwa

k. Mkwanguliro (epilogue)

Mawu otsiriza omwe amapezeka kumathero kwa nkhani zamchezo ndi zolemba monga nthano yayitali, sewero kapena ndakatulo yayitali ndipo nthawi zambiri amakamba za phunziro la m'nthano kapena sewero.

l. Mpanduki (foil)

Mpangankhani yemwe ntchito yake n'kusonyeza kapena kutsindika kakhalidwe kake kotsutsana ndi ka mpangankhani wina

m. Msemphano (irony)

- Kuyankhula mawu onena zina ukutanthauza zina. Msemphano uli ndi mitundun iyi:
- Msemphano wa mawu pomwe mpeki amanena zina akutanthauza zina
- Msemphano wa mchisudzo pomwe owonera amatulukira zinthu zomwe mpangankhani sakuzidziwa
- Msemphano wa momwe zinthu zilili pamene pamakhala kusiyana pakati pa zotsatira zoyembekezeka ndi zotsatira zenizeni

n. Nunsu ya chisudzo (scene)

Tsatanetsatane wa zochitika m'kagawo ka gawo lachisudzo. Nthawi zambiri nunsu za chisudzo zimakhala ngati nthambi za magawo akuluakulu a sewero

o. Kudziyankhulitsa (soliloque)

Zoyankhula za m'sewero zomwe zimapereka chithunzithunzi cha malingaliro ndi maganizo omwe woyankhulayo ali nawo ndipo woyankhulayo amakhala ali yekha.

p. Kuchita chisudzo mwachinunu (miming)

Kuchita chisudzo mwachinunu pogwiritsa ntchito manja ndi kusinthasintha maonekedwe a nkhope

CHAMDOTHE NDI ZISUDZO ZINA

MUTU 1: CHAMDOTHE

Wolemba: (Mufunanji Magalasi)

Womasulira: (Wisdom Nkhoma)

Ochita chisudzo

1. Chamdothe

Mwana wa mayi Ndatopa yemwe adaumbidwa ndi dongo pamene mayiyo ankafunitsitsa atakhala ndi mwana. Ankadana kwambiri ndi Kaziputa ngakhale kuti iyeyu (Chamdothe) sankamuyamba ndipo analibe mangawa. Ankakondana kwambiri ndi Zione mwakuti ku masewera a masanje adamusankha kukhala mkazi wake. Ankadziwa kuti mdani wake wamkulu ndi mvula komanso madzi mwakuti sankakhudza madzi ndipo mabingu akayamba kumveka amathawira kunyumba kwa amake. Adanyowa ndi mvula pamene ankathawira kwa mayi ake pochokera kocheza ndi Zione ndipo thupi lake lidawolowa mpaka kugumuka.

2. Ndatopa

Mayi a Chamdothe komanso mkazi wa Angozo yemwe analibe mwana. Anali Msena ndipo adachita kulowoledwa. Mayiyu anali mzawo wapamtima wa mayi Lunda. Adapita kwa sing'anga komwe adapatsidwa mankhwalu oti amuthandize kuti akhale ndi mwana. Mamuna wake adachoka nkumapita ku Chiromo ndipo iye (Ndatopa) adazindikira kuti akukapeza mkazi wina kuti abereke naye ana. Adanamiza mnzawo, Mayi Lunda kuti akumva mutu

chonsecho akaomba mwana m'nyumba. Ankaganizira kwambiri za kusabereka kwake mwakuti atatopa adaumba mwana wadongo ndipo adapempha Chiuta kuti ampatse mwana. Mwana wadongoyo adakhala ndi moyo ndipo ankamukonda komanso ankamuteteza kwambiri. Mabingu akayamba ankamuyimbira nyimbo ya "Kamdothe thawa mvula" kuti asanyowe n'kufa.

3. Angozo

Mamuna wa Ndatopa yemwe adakangana ndi mkazi wake popeza sankaberekera ana. Adachoka pakhomu napita kunyanja ku Chiromo komwe mkazi wake ankakhulupirira kuti amakapezako mkazi wina woti abereke naye ana.

4. Mayi Lunda

Mnzawo wapamtima wa mayi a Chamdothe. Ankavina limodzi gule wa bongololo. Ankakonda kumuyendera mnzawo, Ndatopa, ndipo tsiku lina adadabwa atapeza Ndatopa atadzitsekera mnyumba. Ankamvetsa vuto la mnzake ndipo anali kumulimbikitsa kuti asamakhale ndi nkhwana.

5. Zione

Mtsikana yemwe ankagwirizana kwambiri ndi Chamdothe ndipo adagwa naye m'chikondi. Adapereka mphatso ziwiri kwa Chamdothe: chibangiri komanso nkhanu. Ankamutezeza Chamdothe kuti asakhudze madzi. Kaziputa ndi Chamdothe ankamulimbirana. Kaziputa adamuyamikira kuti anali wokongola wosayenera kukhala mkazi wa

Chamdothe. Adachititsa kuti Chamdothe avumbwe n'kusungunuka mpaka kufa ndi mvula.

6. Kaziputa

Mnyamata wamavuvu yemwe sankagwirizana ndi anyamata komanso atsikana. Ankakonda kumuvutitsa Chamdothe kosewera. Adamunyoza Chamdothe kuti ndi chidzete popeza ankayimba nyimbo zachisoni komanso adatafuna khala. Ankamufuna kwambiri Zione ngakhale kuti Zioneyo anakondana ndi Chamdothe. Adatenga mbuzi yomwe adaumba Chamdothe nkuyinyenyera m'madzi. Adamuza Chamdothe kuti Zione ngokongola mwakuti sakadakhala mkazi wamunthu ngati iyeyo (Chamdotheyo).

7. Dama

Mnyamata wansangala yemwe amapezeka kumasewera komwe ankapita Chamdothe. Adayetsa kuti Chamdothe ndi Kaziputa ayanjane powakumbutsa kuti anali kuchita masewera chabe. Adalanditsa Chamdothe pamene Puna ndi Kaziputa ankamukankhizirana.

8. Lunda

Mnyamata wina yemwe ankamukonda Chamdothe ndipo adamulandira kukhala mzawo. Adaopseza Kaziputa kuyi asachitire mavuvu munthu wam'mudzimo. Akadangoyerekeza ndiye kuti iye ndi onse am'gulu lake akadathesemulidwa.

9. Puna

Mtsikana yemwe ankagwirizana ndi Kaziputa ndipo pamasewero a amayi ndi abambo anali mkazi wake.

Kaziputa damukana mochititsa manyazi ku Mnjiri ngakhale anali bwenzi lake. Ankathandiza Kaziputa kumuvutitsa Chamdothe.

10. Anyamata ndi atsikana am'mudzi

Ankakhala nawo ku masewero osiyanasiyana omwe ankachitika m'mudzimo.

Malo mwachidule

1. Kubwalo lamasewero m'mudzi

- Komwe anyamata ndi atsikana amakonda kukasewera m'mudzi usiku ngakhale masana
- Azimayi ankapitako kukamvina magule osiyanasiyana monga gule wa bongololo.

2. Kunyumba kwa Ndatopa

- Komwe kunkachikira mkangano pakati pa Ndatopa ndi Angozo mamuna wake
- Ndatopa adaumba mwana wadongo, Chamdothe

3. Kumunda

Chamdothe ndi amake adapitako koma adathawa mvula nalolera kusiya makasu ndi dengo pofuna kupulumutsa moyo wa Chamdothe.

4. Ku Mnjiri

Komwe Kaziputa adamukana Puna ngakhale anali bwenzi lake

5. Kunyanja ku Chiromo



Komwe mamuna wake wa Ndatopa, Angozo, adasamukira pambuyo pokangana ndi mkazi wake pankhani ya kusabereka

6. Kumtsinje

Komwe Kaziputa adatenga mbuzi yomwe Chamdothe adaumba nayamba kuyigumbula mwendo umodzi umodzi mpaka adayitayira m'madzi n'cholinga chofuna kumuyesa Chamdotheyo

NUNSU YOYAMBA

Kaziputa anyoza Chamdothe

Kaziputa adakumana ndi Chamdothe pabwalo lasamasewero ndipo adamunyoza kuti ndi opusa ndi anzake onse popeza

- a) ankachita masewero omvetsa chisoni.
- b) amayimba nyimbo zomvetsa chisoni pamene anthu ena onse anali kusangala.
- c) amadziyerekeza ndi birimankhwe wobwretsa imfa.
- d) anthu ochenjera sachita masewero okamba za imfa.

Kaziputa adapeperetsa Chamdothe pomuza kuti atafune khala nkunena kuti ngochenjera ndipo akatero adzasiya kumunena kuti chidzete. Chamdothe adatsomphola khalalo nkulitafuna koma adatsamwa nalo. Kaziputa adaonjezera mnyozo wake pomunyodola Chamdothe kuti anthu ochenjera sadya makala. Chamdothe adakwiya mwakuti pamene Kaziputa amachoka pabwalo adamutsatira ngakhale Dama ankamuletsa.

Kumbutso: Chamdothe adauza Kaziputa kuti gulu lawo limaonetsa chisangalalo poyimba nyimbo zachisoni choncho kuyimba nyimbo zachisoni sikudali kupusa.

Kunja kudayamba mabingu ndi ziphaliwali ndipo Dama adauza anzake kuti mvula idayenera kugwa panthawiyi. Chamdothe, pozindikira mavuto ake monga mwana wadongo, adayamba kuthawira kwawo. Panthawiyi, mayi ake a Chamdothe ankamuyitana ndi nyimbo ya “Chamdothe thawa mvula.” Zione adamunyengerera Chamdothe kuti asapite kwawo popeza anali kusewerabe. Chamdothe atafika kunyumba adafuna kudziwa kuchokera kwa amayi ake kuopsa kwa kuvumbidwa ndi mvula. Ndatopa, mayi ake, adamufotokozera kuti iye anali wosiyana ndi anthu enawo popeza adachita kuombedwa ndi dongo choncho sakuyenera kukhudzidwa ndi dontho lamvula: angadzabwerere ku dongo komwe iye adachokera. Iye adali ndithu mdani wamvula yomwe idali imfa yake.

Maphunziro m'gawoli

a) Chikondi/Chilungamo/Kuteteza

Ndatopa adamuza mwana wake Chamdothe kuti adapangidwa kuchokera ku dongo choncho adayenera kumathawa mvula yomwe ikadatha kumupha. Mayiyu adafotokozera mwana wake momveka bwino za umoyo wake ndipo tsiku lina ataona kuti kunja kwayamba mabingu ndi ziphaliwali adayamba kumuyimbira kanyimbo

komuyitanira kunyumba kuti tsoka lisampeze popeza mwana adali yekhayo.

b) Chidwi

Chamdothe adafuna kudziwa chomwe mayi ake ankaopa pomuyitana ndi nyimbo kuti athawe mvula(N'chifukwa chiyani anayenera kumathawa mvula?).

c) Kunyoza

Kaziputa adanyoza Chamdothe ndi anzake kuti anali opusa poeza amayimba nyimbo zomvetsa chisoni pamene ena onse ankasangalala.

d) Ulemu

Chamdothe adavomera kuyitana kwa amayi ake ndipo adapita mwachangu ngakhale Zione ankamunyengerera kuti anali kusewerabe.

NUNSU YACHIWIRI:

Kubadwa kwa Chamdothe

Ndatopa adaloleza Chamdothe kuti apite akasewere ndi anzake. Ndipo pambuyo pake Mayi Lunda adabwera kudzacheza ndi mayi a Chamdothe. Mayiwa adampeza mnzawoyo ali m'malingaliro ndipo atamufunsa adati ankakumbukira ubwana wawo. Azimayi awiriwa adavinira limodzi gule wa bongololo ndipo Mayi Lunda adanyamuka n'kumapita. Ndatopa adakumbukira mkangano womwe udachitika ndi mamuna wake Angozo pankhani yakusowa

mwana ndipo udachititsa kuti mamunayo asamuke pakhomo. Ndatopa adakumbukira zinthu zotsatirazi:

- a) Angozo adamutcha Ndatopa buthu popeza adalibe mwana.
- b) Abale a Angozo ankamufunsa mafunso ambirimбири ndipo asuweni ake aakazi ankamunena kuti adangodzivutitsa kupeza mkazi.
- c) Angozo ankati anzake ankamunena kuti Kalulu adamudutsa m'mphechepeche.
- d) Ndatopa adauza Angozo mamuna wake kuti ankamwabe mankhwala omwe awiriwa adakatenga kwa ng'anga ina.
- e) Angozo ankafuna kutenga mkazi wina kuti amuberekere ana.
- f) Angozo adamulowola Ndatopa kwa Asena.

Mkangano umenewu udachititsa Ndatopa kuganiza zongoomba chidole ndi dongo ndipo adakatapadi dongolo nadzitsekera m'nyumba mwakuti pamene Mayi Lunda adabera kudzacheza, sadatsekule chitseko. Adamunamiza mnzawoyo kuti anali kumva mutu koma pomumvetsa Ndatopa, Mayi Lunda adamuza kuti amuna amalemekeza mkazi akawaberekera ana ndipo kuti ngati mkazi satero amakhala wopanda pake. Ngakhale mayiyu adayetsa kunyengerera Ndatopa kuti amutsekulire aone mbiya yomwe amaomba, iye sadatsekule. Ndatopa adauza Mayi Lunda kuti awayitana akatsiriza kuomba mbiyayo popeza anali atangoyamba kumene ntchitoyo.

Panthawiyi Ndatopa akusisima adaomba chidole ndipo adapempha Chiuta kuti ampatse mwana. Adatsinzina nakweza manja kumwamba kwa Mulungu ndipo chidolecho chiodakhala ndi moyo. Mayi Lunda ankadikirabe panja panyumbayo koma Ndatopa adawauza kuti anali asadatsirizebe kuomba ngakhale mphika umodzi.

Chamdothe, mwana yemwe anali atangoombedwa chakumene ndipo adapatsidwa moyo, adayamba kuyankhula pofunsa za mayi yemwe anali kunja kwa nyumbayo koma mayi ake adam'phimba pakamwa kuti Mayi Lunda asamumve. Pambuyo pake Ndatopa adauza Mayi Lunda kuti awapititsira kwawo miphika yomwe anali atangotsiriza kumene kuomba ndipo ayinyamula mosamala.

Kumbutso: Mayi Lunda ndi omwe adaphunzitsa Ndatopa kulotcha mimphika.

Chamdothe pabwalo tsiku loyamba

- a) Kaziputa adafuna kuti amudziwe Chamdothe ndipo adazizwa atamva kuti ndi mwana wa Ndatopa popeza adauzidwa kuti Ndatopa sakadakhala ndi mwana ndiponso analibe mwamuna.
- b) Puna adaonjeza kuti Ndatopa akadakhala ndi mwana sakadakula anthu osadziwa.
- c) Chamdothe adauza Kaziputa kuti amake adamtenga kubanja lina m'mudzi wa Kuserikumvenji.

- d) Puna ndi Kaziputa sadakhulupirire ndipo adayamba kumukankha Chamdothe kuti anene zoonza koma Lunda ndi Zione adaleretsa. Lunda adaopseza Kaziputa ndipo Chamdothe adapeza mwayi wothawira kwa amayi ake.

Chamdothe adafotokozera mayi ake zomwe ankanena Kaziputa ndi Puna kuti iwo alibe mwana komanso mudzi wa Kuserikumvenji kulibe. Ndatopa adachenjeza Chamdothe kuti asamawandikire anthu awiriwa angadzamuphetse. Adamuuzanso kuti asamale ndi Kaziputa popeza anali ndi mavuvu ndipo Ndatopa sakadatha kumuteteza kumavuvuwo. Ngakhale Chamdothe adanena kuti ankafuna kukhala ngati mnyamata wina aliyense pophunzira mavuvu n'kuwagonjetsa popeza mamuna aliyense amatero kuti akule, Ndatopa adamuuzanso kuti sanayenera kuchita masewero onyansawo kuti akule. Chamdothe adauza amakewo kuti Zione, Dama ndi Lunda adamulandira kale ngati mnzawo kubwalo. Ndatopa adamuchenjeza kuti anzakewo asamupititse koopsa.

Chamdothe agwa m'chikondi ndi Zione

- a) Adakangana ndi Kaziputa popeza ankati Zione ndi wake (mkazi wa Kaziputa) ndipo adamutsimikizira kuti tsopano ndi mkazi wake (wa Chamdotheyo).
- b) Adalandira chibangiri kuchokera kwa Zione.

Matanthauzo amawu

- a) Mavuvu

Khalidwe lochita zinthu mosaugwira mtima,
modzionetsera komanso moonjeza.

b) Gwetseranani mumchenga

Siyani kukangana ndipo yanjani.

c) Chibangiri

Khoza lachitsulo lovala kumanja makamaka akazi

Mgiwirzano wa mayina ndi nkhani

a) Chamdothi

Mwana wadongo –adachita kumbidwa ndi mayi ake kuchokera ku dongo. Zinthu zoumba ndi dongo zimasungunuka ndi madzi. pachifukwachi Ndatopa, mayi a Chamdothe anali pantchito yoonetsetsa kuti mwanayu asakhudze madzi ndipo adamulangiza motsindika kuti mvula ndi mdani komanso imfa yake.

b) Kaziputa

Mnyamata woputa dala anzake- adali wamavuvu ndipo nthawi zambiri ankamuputa dala ndikumamvutitsa Chamdothe. Mnyamatayu ankamunyoza kwambiri Chamdothe kuti anali chidzete.

c) Ndatopa

Mayi wotopa/wolema: Adalemba ndi kusakhala ndi mwana nkumavutana ndi mamuna wake, Angozo mwakuti adaomba mwana wadongo ndipo adapempha Mulungu kuti ampatse mwana. Chidole chomwe adaombacho chidakhaladi mwana, Chamdothe.

d) Zione

Ona zinthu monga zabwino ndi zoyipa zomwe: Pamene Chamdothe adamkonda mtsikanayu adayenera kukonzekera kuona zinthu zabwino ndi mavuto ndipo adakumana nawodi. Poyamba adavutitsana ndi Kaziputa polimbirana Zioneyo komanso kumapeto adanyowa nasungunuka n’kufa kamba ka Zione. Pambali pa zinthu zoyipazi, Chamdothe adatetezedwa komanso adakondedwa ndi Zione. Iye adalandira mphatso ziwiri kuchokera kwa Zione: chibangiri koamnso nkhanu.

Maphunziro m’gawoli

a) Nkhanza

Kaziputa ndi Puna adayamba kumukankhizirana Chamdothe pamene ankamutsutsa zoti sadatengedwe ku banja lina ndipo mudzi wotchedwa Kuserikumvenji kudalibe.

b) Kuteteza

Zione ndi Dama komanso Lunda adamuleretsa Chamdothe pomuza Kaziputa kuti iye amangodana ndi Chamdothe ndipo adaonjezanso kuti asayerekeze kumuvutitsa Chamdothe. Adamuopsezanso kuti mavuvu akewo asachitire munthu wam’ mudzimo popeza akatero adzathesemulidwa.

c) Chikondi

Chamdothe ndi Zione adagwa mchikondi. Chamdothe adauza Kaziputa, ngakhale anali wamavuvu, kuti Zione ndi mkazi wake. Zione adapereka chibangiri kwa Chamdothe.

d) Kukanika kulongosola



Kaziputa adakanika kumufotokozera Chamdothe pamene adafuna kudziwa ngati iyeyo (Kaziputa) anli kuonetsera chikondi chake pa Zion pamene adanena kuti ndi mkazi wake.

NUNSU YACHITATU

Chamdothe kumtsinje ndi kumunda

a) Kumtsinje

Chamdothe adaomba mbuzi yadongo n'kumasewera nayo. Kaziputa adamulanda mbuziyo ndipo adapita nayo pamwala womwe unali pakati pa dziwe. Kaziputa adauza Chamdothe kuti ankafuna kuona ngati Chamdothe angapulumbutse mbuziyo. Adayigumula nayiponyera m'madzi. Zion ndi anzake ena adamuthamangira Chamdothe yemwe panthawiyi ankayenda m'mbali mwa mtsinje posafuna kuti alumphire m'madzi. Zion adauza Chamdothe kuti Kaziputa adachitira dala kugumula komanso kuponya m'madzi mbuzi yake pofuna kulipsira zomwe Chamdothe adachitira Puna usiku wina. Zion adakumbutsa Chamdothe kuti Kaziputa amachitira anzake zoipa ngakhale asadamuyambe. Kaziputa adakana Puna ku Mnjiri. Pochoka kumtsinjeku, Zion adampatsa Chamdothe nkhanu kuti akapereke kwa amayi ake popeza adakhala nthawi asadazilawe. Pochoka pamalopa Chamdothe adaganizira zinthu ziwiri zotsatirazi:

- i. Chomwe chinkamuchititsa Kaziputa kuti azimusungira nkhwidzi nthawi zonse
- ii. Adalakalaka Zion atadzakhala mkazi wake

b) Kumunda

Chamdothe adauza amake kuti adaganiza zopita nawo kumunda popeza sankafunanso kusewera panthawiyi. Ndatopa adafuna kudziwa kuchokera kwa mwana wake Chamdothe chomwe Zion adalinga popereka nkhanu kwa Chamdothe. Mwanayu adayankha amakewo kuti Zion adati nkhanuzo ndi zawo(za amakewo) osati za iyeyo. Mafunso omwe Chamdothe adaponyera Ndatopa adasonyeza kuti iye (Chamdothe) adagwa m'chikondi ndi Zion ngakhale kuti sadam'thule dzina.

Adakacheza choncho, Ndatopa adagwira nkhumu yomwe panthawiyi inkapereka zinthu ziwiri: chakudya chokoma komanso macherechete. Pamundapa, Chamdothe ndi mayi ake, Ndatopa adacheza motere:

- a) Ndatopa adakana kumuza Chamdothe nyimbo ya macherechete komanso ya nkhumu.
- b) Ndatopa adauza Chamdothe kuti akadatha kugonetsa nkhumu m'kakhola ndi kuyimba nyimbo yekha.
- c) Chamdothe adayankha kuti kutero ndi kuchitira nkhanza tizilombo monga nkhumu.
- d) Ndatopa adatsimikizira Chamdothe kuti nkhumu zidalengedwa kuti zizidyedwa.
- e) Ndatopa adadziwitsa mwana wakeyo kuti anthunso adzafa ndipo uthenga wa imfa udabwera ndi namzikambe kuchokera kwa Chiuta kupita kwa Mchewa kapena Mmaravi wamamuna ndi wamkazi pa Kapirimtiwa koma Chamdothe adayankha kuti nkhumu/chilule siziyenera kuphedwa kamba ka uthenga wa imfa womwe udabwera

ndi namzikambe popeza ndi tizilombo tating'ono ndipo imfa yake njopanda pake.

f) Ndatopa adauza Chamdothe kuti imfa zisankha ndipo sifotokoza chifukwa chake.

Asanatsirize macheza pamundapa kudamveka mkokomo wamvula kotero Ndatopa adamutenga Chamdothe nkuthawira naye kunyumba kuti asanyowe. Adasiya makasu ndi dengi.

Maphunziro m'gawoli

a) Chikondi

Ndatopa adacheza ndi mwana wake ndipo adamufotokoza chiyambi cha imfa komanso adamuuzako za nkumbi nampangira macherechete.

Zione adapereka nkhanu kwa Chamdothe kuti akawapatse mayi ake popeza adakhala nthawi yayitali asadazilawe.

Zione adamuthamangira Chamdothe, pamene adamuona akuyenda m'mbali mwa mtsinje, kuti asagwere m'madzi.

b) Kuteteza

i. Zione adamuthamangira Chamdothe, pamene adamuona akuyenda m'mbali mwa mtsinje, kuti asagwere m'madzi.

ii. Ndatopa adalolera kusiya makasu ndi dengi pamunda pofuna kupulumutsa Chamdothe ku mvula yomwe ikadamupha.

Matanthauzo a mawu

Nkhumbi

Kachirombo kooneka moyerera komwe kamakhala ndi mapiko olimba ndipo anthu amapangira mangwere.

Macherechete

Choyimbira chopangidwa ndi chingwe chachitali chomwe anthu amatungirako mapiko a nkumbi akunja navala m'khosi mokupatira, kenaka namayimba ndi zala.

NUNSU YACHISANU

Imfa ya Chamdothe

Zione adapita kwa mayi a Chamdothe ndipo adawapempha kuti amutenge akasewere naye. Mayi a Chamdothe adamukaniza pomuza kuti samafuna zoti mwana wawo Chamdothe akasewere kutali popeza nyengo yamvula inali itafika. Zione adalonjeza kuti akamudyetsa komanso akamusamalira bwino Chamdothe. Ndatopa adamuloleza Zione kuti amutenge Chamdothe.

Zione ndi Chamdothe atafika pabwalo posewerera, Kaziputa adasiya Puna nanyamuka kuti akamukankhe Chamdothe koma Dama ndi Lunda adaleretsa. Mkangano wolimbirana Zione udabukanso pakati pa Chamdothe ndi Kaziputa motere:

a) Chamdothe adauza Kaziputa kuti adali kale ndi Puna chonchon anayenera kukhala ndi Punayo basi.

b) Chamdothe adaonjezanso kuti n'kutheka kuti Kaziputa anali woyipa n'chifukwa chake Zione adasankha Chamdotheyo.

- c) Kaziputa adamuza Chamdothe kuti sakhalitsa naye Zione.
- d) Kaziputa adamuuzanso mnzakeyu kuti Zione ndi mtsikana wokongola choncho sangakhale mkazi wa Chamdothe.

Dama adalowerera mkanganowu ndipo adauza Chamdothe ndi Kaziputa kuti sadayenera kukanganirana Zione popeza awa adali masewera chabe (zamasanje). Zikadakhala zenizeni, makolo sakadawaloleza kuti azisowa kwa kanthawi. Kaziputa adamuyankha Dama kuti mudali zambiri m' masanje zoposa kungosewera za amayi ndi abambo.

Macheza otsiriza a Chamdothe ndi Zione

- a) Zione adafuna kudziwa chomwe chidamuchititsa Chamdothe kuti amusankhe kukhala mkazi wake. Chamdothe adamuyankha kuti mwina ndi maphikidwe ake abwino abowa komanso adalawa nkhanu zake.
- b) Zione adatsutsa ganizoli ponena kuti nkhanuzo adaphika sanali iyeyo.
- c) Zione adafuna kudziwa ngati Chamdothe adawauza mayi ake za chibangiri chomwe Zione adamupatsa koma Chamdothe adati sadwauze amake popeza ankasowa poyambira. Nkhaniyi idakwiririka ndi nkhanu inzake yokhudza kaliyoliyo yomwe Zione ankati amuuzabe Chamdothe panthawi yopuma.
- d) Kunja kudamveka mabingu ndipo Chamdothe adatsanzika Zione kuti azipita koma Zione adamuza kuti anali asadayimbe chimbo yotsekera masanje .

- e) Zione adamuza Chamdothe kuti abisala m'nyumba yamasamba koma iye adamuyankha kuti nyumba yamasambayo singamuteteze.

Mayi a Chamdothe, Ndatopa, adayamba kumuyitana kudzera m'nyimbo ya “Chamdothe thawa mvula.” Zione adathamanga ndi Chamdothe kuti akamusiye kwawo koma mnyamatayu adayamba kuwolowa n'kumachoka chiwalo chimodzichimodzi mpaka udatsala mutu wokha womwe udagwera panso pamene Zione amawupereka kwa Ndatopa, mayi a Chamdothe.

Maphunziro m'gawoli

a) Kusasamala

Zione ankadziwa kuti Chamdothe sayenera kukhudza madzi akadafa nawo koma adalolera kumuchedwetsa pamene mvula inkayamba n'kumathamanga naye pamvula mwakuti adanyowa, adasungunuka ndipo imfa yake idali yomweyo.

b) Kudziyenereza

Kaziputa adauza Chamdothe kuti Zione anali mkazi wokongola wosayenera kukhala mkazi wa Chamdothe koma iyeyo.

c) Kudziteteza

Chamdothe atamva mabingu adadziwa kuti mdani wake, mvula, wayandikira ndipo adatsanzika Zione kuti azipita kwawo ndipo pamene Zione adamuza kuti akabisala panyumba yamasamba, Chamdothe adamuyankha kuti nyumba yamasamba singamuteteze ku mvula.

Mawu ena ofunika kuwaunikira

1) Chamdothe ankakhala moyo wosasangalala kwenikweni

- a. Nthawi zambiri ankavutitsidwa komanso kunyozedwa ndi Kaziputa.
- b. Nthawi zonse ankakhala mwa mantha makamaka poganizira kuti mdani wake wamkulu ndi madzi.
- i. Kaziputa atamutengera mbuzi yake yadongo n’kupita nayo pamwala pakati pa mtsinje iye adamulondola koma ankayenda m’mbali mwa mtsinje poopa kuti anganyowe ndipo anzake adamuthamangira nkumugwira kuti asalumphire m’madzi.
- ii. Kunja kukaonetsa zizindikiro zoti mvula igwa iye amathawira kwawo mvulayo isanayambe poopa kuti anganyowe n’kugumuka.

2) Anthu anali kuchitira nkhanza anzawo

Mamuna wake wa Ndatopa, Angozo, adamunena mkazi wake kuti ndi buthu ndipo adachoka pakhomo n’kumapita kunyanja ku Chiromo popeza mkazi wakeyo sankabereka ana ngakhale kuti anthuwa sankadziwa kuti vuto lidali ndi yani kwenikweni.

3) Fisi ali ndi bwenzi

Kaziputa anali munthu wamavuvu komanso woyamba dala anzake komabe anali ndi bwenzi lake Puna amene amachita naye zinthu nthawi zambiri ndipo kumasewero amasanje anali mkazi wake.

- a) Ndatopa adanyozedwa ndi mamuna wake Angozo pamene sankabereka komabe Mayi a Lunda ankamumvetsa ndipo ankayesetsa kuti asmakhale ndi nkhawa.

MUTU 2

KHOSWE WAPADENGA

(Smith Likongwe)

Ochita chisudzo

Bonzo ndi Jubeki

Akamberembere omwe adakhala akuchita za umbanda kwa nthawi yayitali. Adadumphira mpanda nathawa kundende ndipo pothawapo adathyola nyumba ya woyang’anira akayidi kundende nkubamo zovala zachimuna zomwe ankafuna kuti asinthire poopa kugwidwa. Anthu awiriwa adaulula ubwenzi wa Khoswe ndi Anne ku bwalo la milandu pamaso pa mkazi wa Khoswe ndi Goli.

Khoswe

Woyang’anira akaidi kundende wabodza yemwe ankazemberana ndi mkazi wa mkulu wapolisi. Adanamizira kuti ankatsekula m’mimba pamene akaidi awiri, Bonzo ndi Jubeki, adathawa kundende. Adanamanso kuti akaidiwo adamulanda yunifolomu komanso adanama mukhothi kuti mkazi wa Goli samudziwa.

Goli

Mkulu wapolisi (Insipekitala) yemwe mkazi wake anali pa ubwenzi wamseri ndi Khoswe. Ankakonda ntchito yake.

Adagwira Bonzo ndi Jubeki pamene mlonda wina adamutchayira lamya yomuuza za kupezeka kwawo pamalo olakwika usiku.

Anne

Mkazi wa Goli komanso bwenzi lamseri la Khoswe Khoswe yemwe anali wabodza ndithu. Adanamiza mamuna wake kuti akuba adaswa zenera iye akugona ndipo akumulota mamuna wakeyo chonsecho kuba kudachitika iye akucheza ndi bwenzi lake Khoswe m'chipinda m'nyumba momwemo.

Mlonda

Adathandiza apolisi kuti agwirensa Bonzo ndi Jubeki powatchayira lamya.

Apolisi asanu

Adazinga malo omwe panali Bonzo ndi Jubeki.

Woweruza milandu

Anthu omvera milandu

Malo mwachidule

Kunyumba kwa Goli

Kundende

Kunyumba kwa mzimayi wogulitsa mowa

Kumanda komwe kudabisidwa ndalama

Panjira (pamene Bonzo ndi Jubeki adasinthira zovala)

Kubwalo lamilandu

Kunyumba kwa Khoswe

Kunchito kwa Goli

NUNSU YOYAMBA

Bonzo ndi Jubeki athawa kundende

Chomwe zidachititsa kuti Bonzo ndi Jubeki amangidwe

- Adathyola banki ndipo adaba ndalama zambiri

Zomwe zikadachititsa kuti Bonzo ndi Jubeki agwidwe

- Ganizo la Bonzo loti pothawa kundende avale nsapato: mdidi wawo ukadamveka
- Mkuwo wa Bonzo ataponda msomali: atajowa mpanda, Bonzo adakafikira kuponda msomali ndipo adalira ngati mwana wamng'ono

Kusiyana kwa Bonzo ndi Jubeki ndi Nyapala pamilandu yawo

- Bonzo ndi Jubeki adathyola banki naba ndalama zambiri; choncho adali akaidi abwinoko.
- Nyapala adagwirira kamwana kakang'ono choncho anali mkaidi wachabechabe.

Maganizo a Bonzo ndi Jubeki pa chitetezo cha ndalama zomwe adabisa

- Bonzo anali ndi chikaiko ngati ndalama zomwe adaba nkubisa kumanda zidalipobe popeza panali patapita zaka ziwiri chikwirireni ndalamazo choncho china chake chikadatha kuchitika.
- Jubeki adatsindika kuti palibe yemwe akadawadziwa malowo popeza anthu adasiya kugwiritsa ntchito mandawo.
- Bonzo adatsimikiza nawo mfundoyi ponena kuti palibe yemwe akadadziwa malo omwe anali



pamtunda wa masitepe 77 kuchokera pamtumbira wotsiriza komanso palibe yemwe akadakumba kumanda.

- Jubeki adakayikira zinthu zotsatirazi:
 - ✓ Munthu akadatha kuswa mphanje kapena kutsekula munda pamalopo.
 - ✓ Munthu akadatha kumangapo nyumba.

Ngakhale Jubeki anali ndi nkhawa zimenezi, adalinsu ndi chikhulupiro kuti zimenezi sizingachitike kumanda

Umboni woti Bonzo ndi Jubeki adali oopsa komanso adachita umbanda ndi umbava kwa nthawi yayitali

- Paulendo wothawa kundende, ngakhale munali mumtima, Jubeki adakwanitsa kudziwa cinthu choopsa chomwe chinali patsogolo pawo chomwe chikadatha kuwavulaza monga dzenje.
- Jubeki adathawapo apolisi chipolopolo chili pantchafu apolisiwo atamuwombera.
- Jubeki adagwira ntchitoyi (umbava ndi umbanda) kwa zaka zoposa makumi awiri.
- Bonzo adagwira ntchitoyi kwa zaka khumi ndi mphambu zisanu ndi ziwiri.

Zomwe Bonzo ndi Jubeki adayenera kuchita asazindikiridwe komnso asagwidwe

Adayenera kupeza zovala zina mwachangu popeza Malaya akundende omwe anali atavala panthawiyi akadagwidwa nawo poti ngakhale munthu wongodziyendera akadatha kuwadabwa nkuwagwira.

Kumbutso

- Bonzo ndi Jubeki adagwirizana zokathyola nyumba yomwe adayiona pafupi n'kulowa kuchipinda cha makolo kuti akapeze zovala zachimuna.
- Jubeki adauza Bonzo kuti Nyapala adali wopusa zedi popeza adagwirira mwana pamene azimayi adalipo ambirimbiri omwe akadatha kuwafunsira.
- Kugwirira ana ndi ufiti ndipo anthu amachita zimenezi pofuna zizimba.

Zipangizo

1. Zining'a

- a. titaya bomwetamweta: titaya mwayi wopezapeza
- b. tinapakula : tinaba
- c. walasa : walunjika pa zomwe ndimaganiza
- d. kamatekenya : munthu wamatekenya

2. Zifanifani

- a. Unafuula ngati mwana wamng'ono
 - Unafuula mokweza kwambiri kamba ka ululu.
- b. Ukuyenda ngati kamatekenya
 - Ukuyenda motsimphina kamba ka ululu wakuphazi.

3. Chifaniziro/Chizindikiritso

- Misomali ndi mayenje
- Chizindikiritso cha chilango (pothawa kundende adayamba kulandira chilango atangodumphira mpanda)

Chizindikiritso cha kugwidwa (Bonzo ndi Jubeki adayenera kugwidwa- zinthu ziwirizi ndi zina mwa zomwe zikadathandizira kuti agwidwe.)

4. Msemphano

➤ Bonzo ndi Jubeki ndi mbala zoopsa zomwe zathawa kundende koma zinali ndi chikhulupiriro kuti zikapulumuka monga mbala yomwe inapulumutsidwa pamtanda ndi Yesu nthawi yothaitha.

5. Kalosera

• Jubeki adakayikira kuti munthu akadatha kuswa mphanje kapena kutsekula munda pamalo pamene adafotsera ndalama kapena munthu akadatha kumangapo nyumba. Izi zidachitikadi. Pamene anthu awiriwa adathawa kundende adakapeza pamalo pamene adakwirira ndalama patamangidwa chinyumba chachitali.

Maphunziro m'nunsuyi

1. Anthu akuba saopa

Bonzo ndi Jubeki atathawa kundende adaganiza zothyola nyumba ina kuti apeze zovala zina kuti asinthe.

2. Kulimba mtima

- Bonzo ndi Jubeki adathawa kundende.
- Jubeki adathawa apolisi chipolopolo chili pantchafu atamuwombera.

3. Kuganiza mwakuya

- Bonzo ndi Jubeki adaganiza zokabisa ndalama kumanda.
- Bonzo ndi Jubeki adaganiza zoti apeze zovala zina mwachangu poopa kugwidwa ndipo adagwirizana zothyola nyumba ina nkulowa kuchipinda chamakolo kuti akapeze zovala zachimuna popeza kuchipinda kwa ana sakadapeza zomwe amafuna.

NUNSU YACHIWIRI

Ubwenzi wa Khoswe ndi Anne

- Aliyense mwa awiriwa anali pabanja: Anne anali mkazi wa Goli (Insipekitala wa polisi) yemwe ankakhala kunja osati ku layini pamodzi ndi apolisi ena. Khoswe analinso wokwatira.
- Anthu awiriwa amapeza danga locheza pamene mamuna wa Anne, Goli, anali mgulu la anthu okagwira ntchito usiku komanso naye Khoswe amakagwira ntchito yake usiku (kuyang'anira akayidi).
- Macheza awo amachitikira kunyumba kwa Goli usiku.
- Khoswe amakhoteza kunyumba kwa Anne akamapita kuntchito.
- Awiriwa ankalinba mtima nkumacheza mpaka usiku zedi popeza Goli amati akapita kuntchito ankabwerako 7koloko m'mawa ndipo kunali kovuta kuti wapolisi athawire kuntchito.
- Tsiku lina Anne adamuphikira Khoswe zakudya zomwe Khosweyo adaziyamikira mpaka kunyoza mkazi wake ponena kuti Anne pazophika adatha mayunivesite pamene mkazi wake anali adakali ku pulayimale.

Chipwirikiti kunyumba kwa Goli

- a) Akuba adabwera nasolola zovala zomwe zinali pafupi ndi zenera lakuchipinda komwe Khoswe anali kucheza ndi Anne. Akubawa adasololanso yunifolomu ya Khoswe yakuntchito (yunifolomu ya pulizoni).
- b) Khoswe adatchayiridwa thenifolo ndi mzake wakuntchito yomudziwitsa kuti akayidi awiri, Bonzo ndi Jubeki, adathawa.
- c) Anne ndi Khoswe adakanika kufuula kuti apolisi awathandize atazindikira kuti m'chipindamo munabwera akuba poopa kuti akadawululika. Anthu awiriwa ankaopa kuyatsa getsi m'chipinda momwe ankacheza poopa kuti anthu anyumba yoyandikana ndi ya Goli komanso alonda a Goli akadakanena kwa Goli.
- d) Anne adakayikira akayidi omwe adathawa kundende kuti ndi amene adaba zovala kudzera pazenera pamene iye ndi Khoswe adatanganidwa ndi kucheza.
- e) Khoswe adavala zovala za Goli zomwe zidali zazikulu zedi ndipo adatuluka n'kumapita.

Mawu ofunika kuwaona bwino

1. Khoswe analidi khoswe.

- Khoswe ankamuzembera Goli nkumachita ubwenzi ndi mkazi wake Anne chimodzimodzi m'mene amachitira khoswe m'nyumba pozembera mwinyumba n'kumadya katundu wake.

2. Kutchena kapena kukwana kwa zovala ndi pamtendere.

- Khoswe adavala zovala zazikulu zedi zamamuna wake wa Anne popeza adazingwa pamene akuba adathawitsa yunifolomu yake yakuntchito m'mene iye ankacheza ndi Anne m'chipinda mumdima.

Maphunziro m'nunsuyi

1. Chimasomaso

- Khoswe anali pabanja koma anali kuzemberana ndi Anne mkazi wa Goli.
- Anne anali pabanja koma anali kuchita ubwenzi ndi Khoswe yemwe anali pabanja.

2. Mantha

- Khoswe ndi Anne adakanika kuyatsa getsi lam'chipinda momwe ankacheza pamene amafuna kuti ayang'ane zovala za Khoswe popeza anali kuopa kuti anthu oyandikana nyumba ndi ya Goli komanso alonda a Goli akadakamuza bwana wawo.
- Khoswe ankamuopa Goli: ankati ndi wamphamvu zedi mmwakuti akadamugwira ndi Anne mphamvu zonsezo zikadathera pa iyeyo.
- Anne adaganiza zokuwa kuti kudabwera akuba pakutuluka kwa Khoswe m'nyumbamo popeza ankaopa kuti akadawululika.
- Anne ankamuopa mamuna wake Goli. Pamene Khoswe adamuza zoti adzayankhe mamuna wake akabwera pa zakusowa kwa diresi yake yovala pogona komanso zovala za mamuna wakeyo adati asunga mayankho koma adaonjeza kuti Goli monga wapolisi amafunsa mafunso akafukufuku kwambiri.

Matanthauzo amawu

1. Uchidzete : uchitsiru
2. Duwa, nyale, dzuwa, ngale : mkazi wokongola

NUNSU YACHITATU

Kugawana zovala zakuba

- a) Bonzo ndi Jubeki adazindikira kuti zovala zomwe adaba zinali yunifolomu ya wogwira ntchito ku pulizoni komanso diresi yovala pogona.
- b) Jubeki adauza Bonzo kuti iyeyo (Jubeki) ndi yemwe atavale yunifolomuyo popeza adaswa zenera adali iye ndipo kuti Bonzo avala diresi.
- c) Anthu awiriwa adagwirizana kuti yunifolomu yaukaidi ayitaye pobisika poopa kuti kukadakhala kosavuta kuti awalondole.

Milandu ya bonzo ndi jubeki ndi zilango zake

- a) Kuthyola banki, kuba ndalama m'banki komanso kuzimbayitsa ndalama.
- b) Bonzo ndi Jubeki adaba ndalama zokwana K200, 000,000.
- c) Mlandu uliwonse unali ndi zaka zake zoti nthu awiriwa akakhale kundende komanso aliyense mwa iwo adagamulidwa kuti akakhale kundende kwa zaka khumi.

Maphunziro m'nunsuyi

- Kuganiza mwakuya

Jubeki adauza Bonzo kuti yunifolomu yaukaidi ayitaye pobisika popeza kuyitaya pooneka kukadachititsa kuti alondolewe mosavuta.

Zipangizo

➤ Mkuluwiko

M'mphechepeche mwa njovu sapitamo kawiri

Bonzo ndi Jubeki sanayenera kuthyolanso nyumba kuti apeze zovala zina popeza akadatha kugwidwa.

➤ Chining'a

Makhumutcha

Anthu olemera/andalama

NUNSU YACHINAYI

Mkazi wa khoswe adabwa ndi mamuna wake

- a) Anzake a Khoswe adabwera kunyumba namuza kuti mamuna wake sanali kuntchito. Iye adadabwa nazo popeza Mmamuna wakeyo adapita kuntchito komweko atavala yunifolomu.
- b) Mwamuna wakeyo adatulukira kunyumba nthawi yomwe anayenera kukhala kuntchito.
- c) Khoswe adatulukira kunyumba atavala zovala zachilendo: chimalaya chachikulu komanso chibuluku chachikulu.
- d) Khoswe adamuza mkaziyo kuti yunifolomu adamutsomphola akaidi omwe adathawa panthawiye iye ali kuchimbudzi chapanja.

- e) Khoswe adaoneka aodabwa pamene anzake adamuyimbira foni yomudziwitsa kuti akaidi athawa. Abwana a Khoswe ndiwo adamudziwitsa mkaziyu.

Maphunziro m'nunsuyi

a) Bodza

- Khoswe adanamiza mkazi wake kuti iye anali kuntchito, adatsekula m'mimba, anali kuchimbudzi chakunja pamane akaidi ankathawa ndipo akaidiwo adamutsomphola yunifolomu ali kuchimbudziko, chonsecho Khoswe anali kuchibwenzi (kwa Anne) komwe yunifolomu yake idabedwa ndi akaidiwo.

b) Kuopseza

- Khoswe adaopseza mkazi wake kuti amumenya ngati sasiya kumufunsa.

Zipangizo

➤ Zining'a

✓ *Mawu oluma* :mawu aukali

✓ *Mvumbi wazibakera*:zibakera zobwera motsatizana

NUNSU YACHISANU

Zokambirana za Goli ndi mkazi wake

Bodza la Anne kwa mamuna wake Goli

- Adamuza kuti akuba adaphwanya zenera mpaka kuba iye ali mtulo ndipo akumulota iyeyo (Goli). Adaonjezanso kuti apolisi amapereka chitetezo kudziko kusiya okondedwa awo kunyumba.

- Adagwetsa mphwayi mamuna wake pomuza kuti zojambula zidindo za zala za omwe adaba m'nyumbamo angozisiya popeza zipangizo zojambulira zinali zodula.

Mayankho a Goli kwa Anne mkazi wake

- Goli adamuyankha mkazi wakeyo, Anne, kuti kunyumbako adabwerera ntchito komanso kupereka chitetezo ndi ntchito yomwe adafunsira.
- Adatsimikiza zoti atenga zidindo za zala zakumanja za akubawo ndipo monga wapolisi ayesetsa kuti akubawo agwidwe. Adafotokozanso kuti ngati si akaidi omwe adathawa ku pulizoni omwe adaba kunyumbako, adayenera kupeza munthu aliyense yemwe zidindo za zala zake zikadapezeka kuchipindako.

NUNSU YACHISANU NDI CHIMODZI

Bonzo ndi Jubeki agwidwa

- Adafika pamanda pamene adakwirira ndalama zomwe adaba kubanki koma adadabwanataona kuti padamangidwa chinyumba chachitali ndipo sakadakwanitsa kuchigwetsa kuti afukule ndalamazo.
- Mlonda wapamalopo adatchayira lamya apolisi ndipo mkulu wawo (Insipekitala Goli) adatulukira mwamsanga nawauza anthu awiriwa (Bonzo ndi Jubeki) kuti akuwamanga pa mlandu wopezeka malo olakwika usiku.
- Chikhothi cholembedwa "Police" chidathandizira Goli kuti azindikire zoti anthu awiriwa (Bonzo ndi Jubeki) ndi akaidi amene adathawa kundende usiku wapitawo komanso adaba kunyumba kwake.

- Insipekitala Goli adazindikira kuti anthu awiriwa ndi Bonzo ndi Jubeki pamene Bonzo adamunong'oneza namuuzza kuti akadatha kumulemeretsa usiku womwewo ndi ndalama zomwe zidali pa chinyumba chachitalipo.

Kumbutso:

1. Jubeki adagonana ndi bwenzi lake (mkazi wapamalo wogulitsa mowa) mosadziteteza mwakuti anali kukayikira kuti akadatha kumupatsa matenda amakono. Chomwe Jubeki ankadandaula panthawiyi si matenda amakonowo ayi koma kuwululidwa ndi mkaziyo.
2. Jubeki adauza Bonzo kuti akafukula ndalama zomwe adabisa akazisungitsa kwa mkazi wapamalo ogulitsa mowayo.
3. Jubeki adamulonjeza mkaziyo kuti amupatsa ndalama zoti atsegulire malo akeake ogulitsira mowa.

Maphunziro m'nunsuyi

a) Kusasamala

- Jubeki adagonana ndi bwenzi lake (mkazi wapamalo ogulitsirapo mowa) mosadziteteza.

b) Zinthu zazing'ono zimawululitsa zazikulu

- Chikhothi cholemba mawu oti "Police" chidawululitsa Jubeki ndi Bonzo kuti ndi omwe adakaba kunyumba kwa Insipekitala Goli.

c) Chinyengo

- Bonzo ndi Jubeki adanyengerera Insipekitala Goli kuti ampatasa 50 miliyoni Kwacha ngati angawasiye osawamanga.

d) Kukonda ntchito

- Insipekitala Goli adakana kuchita zachinyengo (kulandira ndalama kuchokera kwa Bonzo ndi Jubeki).
- Ngakhale mkazi wake wa Goli adamugwetsa mphwayi kuti zojambula zidindo za zala za omwe adaba kunyumba kwawo angozisiya iye adamutsimikizira mkaziyo kuti iye adabwerera ntchito kunyumbako ndipo ayesetsa kuti okubawa agwidwe.

Zipangizo

a) Chining'a

Akuthirani machaka:

- Akuwomberani ndi mfuni

b) Msemphano

- Anne adauza Goli mamuna wake kuti akuba adaswa zenera iye ali mtulo akumulota mamuna wakeyo chonsecho kuba kudachitika iye atatanganidwa ndi kucheza ndi bwenzi lake Khoswe m'chipinda chomwecho.

NUNSU YACHISANU NDI CHIWIRI

Khoswe apanikizidwa ndi Goli kupolisi

Umboni woti kuthawa kwa akaidi kumamukhudza Khoswe



- Adamizira kuti adadwala mwadzidzidzi panthawi yomwe akaidiwo adathawa koma atafunsidwa ngati adawadziwitsa abwana ake monga mwa dongosolo la pantchito, iye adakana.
- Yunifolomu yake yakuntchito idapezeka kunyumba kwa mzimayi woyendayenda yemwe adapereka zovala kwa Bonzo ndi Jubeki atathawa kundende ndipo chiphaso chake chinali m'tumba lamalaya.
- Diresi yovala pogona ya mkazi wa Goli yomwe idabedwa kunyumba kwa Goli idapezeka pamodzi ndi yunifolomu yake ya Khoswe.
- Zovala zomwe zidabedwa kunyumba kwa Goli pamodzi ndi diresi yovala pogona ya mkazi wake Anne, idapezeka kunyumba ya Khoswe.

Milandu yomwe Khoswe komanso mkazi wake ankaganiziridwa

➤ **Khoswe:**

- Kuthandiza akaidi kuthawa kundende
- Kuthyola nyumba komanso kuba

➤ **Mkazi wa Khoswe:**

- Kuthandizira kuba (kubisa zovala zobedwa m'nyumba)
- Kulephera kukanena kupolisi zakatundu wobedwa yemwe adali m'nyumba mwake.

Maphunziro m'nunsuyi

a) Bodza

- Khoswe adanama kuti adadwala mwadzidzidzi pamene akaidi awiri ankathawa, chonsecho anali akucheza kuchibwenzi kunyumba ya Goli.

b) Chipwirikiti

- Yunifolomu ya Khoswe idapezeka kunyumba kwa mtsikana wapamalo wogulitsa mowa komanso chiphaso chake chidali m'tumba lamalaya.
- Yunifolomu ya Khoswe idapezeka ndi akaidi othawa kundende.
- Diresi la Anne lovala pogona lomwe lidabedwa kunyumba kwa Goli lidapezeka kunyumba kwa mtsikana wapamalo ogulitsa mowa.
- Zovala za Goli zomwe zidabedwa kunyumba kwake, zidapezeka kunyumba kwa Khoswe.

Zipangizo

a) Msemphano

- Goli adauza Khoswe kuti chitsimikizo choti iye (Khoswe) adali ndi akaidi ndi choti atavula yunifolomu yake n'kuwapatsa akaidiwo, iwo adamupatsa malaya ake (a Goli) omwe adaba kunyumba kwake kuti iye asayende maliseche. Zoonza zake n'zakuti akaidi adaba yunifolomu ya Khoswe pamene iye adatanganidwa ndi kucheza ndi Anne m'chipinda chomwe mudabedwamo ndipo Anne ndi yemwe adampatsa Khoswe zovala za Goli kuti avale.
- Mkazi wa Khoswe adaganiziridwa mlandu wobisa katundu wobedwa komanso kulephera kukanena kupolisi zakatundu wobedwa yemwe adali m'nyumba mwake. Zoonza zake n'zakuti zovala za Goli zomwe

zidapezeka m'nyumba mwake sizidabedwe; mamuna wake Khoswe adabwera atavala zovala za Golizo usiku tsono kunali kovuta kuti mkazi wa Khoswe akanene kupolisi.

b) Chining'a

➤ *Ndikuchotsa chimbenene*

- Ndikukhailitsa zedi.

NUNSU YACHISANU NDI CHITATU

Kubwalo lamilandu chilungamo chidziwika

- Mkazi wa Goli, Anne, adauza woweruza kuti adali ali mtulo pomwe akuba adaswa zenera ndipo adazindikira kutacha kuti magalasi anali ataphwanyidwa komanso zovala za mamuna wake zidabedwa pamodzi ndi diresi lake lovala pogona.
- Bonzo adavomereza mlandu wothawa kundende osati wolanda Khoswe yunifolomu. Iye adafotokoza kuti atathawa kundende adaphwanya zenera pa nyumba ina momwe adabamo zovala ndipo adazindikira kuti panali yunifolomu ya msirikali wandende ndi diresi lovala pogona. Pamene ankaba zinthuzi n'kuti bambondi mayi am'nyumbamo akucheza mwachikondi pa kama. Yunifolomu yomwe adatengayo adakasungitsa kwa bwenzi lake ku bala.
- Jubeki nayenso adavomera mlandu wothawa kundende osati wolanda Khoswe yunifolomu. Iye adafotokoza kuti ntchito yake inali yoonetsetsa ngati sikumabwera anthu panthawi yomwe Bonzo amaswa zenera. Nayenso adanena kuti eni nyumbayo anali akucheza pa kama

m'mene iwo ankaba. Iye adati adamuzindikira mkazi wa Goli koma mamuna yemwe annkacheza naye sadamuzindikire.

- Khoswe adauza woweruza kuti akudziwa Bonzo ndi Jubeki osati mkazi wa Goli. Jubeki ndi Bonzo adathawa kundende ndipo adamulanda yunifolomu iye akudzithandiza atadwala m'mimba mwadzidzidzi. Iye adadzikola ponena kuti sadamuone Bonzo pamene amaswa zenera kunyumba ya Goli komanso adakanika kumuyankha Bonzoyo pamene adamufunsa ngati adayamba wajambulitsapo ndi mkazi wa Goli. Khoswe adanenetsa kuti Mayi Goli sanali kuwadziwa.
- Jubeki adawulula kuti sadamutsomphole Khoswe yunifolomu. Iye ndi Bonzo adaba yunifolomu kunyumba ya Goli ndipo m'thumba la yunifolomuyo dapeza chithunzi. Adapereka chithunzicho kwa woweruza milandu. (Khoswe ndi Anne adakumbaturana mwachikondi pachithunzipo.)

Kumbutso:

Goli sankadziwa kuti kunyumba kwake kudalowa mamuna wina yemwe ankazemberana ndi mkazi wake Anne koma zoyankhula za Bonzo ndi Jubeki zidawulula za mamunayu.

Zipangizo

a) Chining'a

- Mumakadzithandiza

b) M'malere/M'biso

- Mlembi sadafotokoze zomwe Goli adachitira mkazi pamene adazindikira kuti anali ndi mamuna wina iye ali kuntchito.

Maphunziro

Kuwululika

Ngakhale Khoswe adayesetsa kuchita bodza kuti ubwenzi wake wamseri ndi Anne usawululike, Bonzo ndi Jubeki adawulula ubwenziwu ku bwalo lamilandu pamaso pa Goli ndi mkazi wa Khoswe.

MUTU 3

MCHIRA WABULUZI

(Enoch S. Timpunza Mvula)

Womasulira: Wisdom A. Nkhoma

Gwero lachisudzo

Mchira wabuluzi womwe udapezeka m'chipanda chamowa womwe Nadzonzi adatenga kwa Nasiwelo ndipo adampatsa mamuna wake Ndileya

Ochita chisudzo

Ndileya

Mamuna wa Nadzonzi yemwe ankamuchita nkhanza mkazi wake. Ankazemberana ndi Nanzunga ndipo ankafuna kumukwatira mwakuti adamugulira nyama yang'ombe kambirimbiri pamene Nadzonzi ndi ana ake anali kudyera mnkhwani. Ankamunyoza Nadzonzi kwambiri.

Nadzonzi

Mkazi wa Ndileya yemwe anali kuchitidwa nkhanza ndi mamuna wake. Anali mtchisi zedi: adatha zaka zitatu osachapa mabulangete, mwezi wathunthu osasesa m'nyumba komanso sankachapa zovala ngakhale mamuna wake ankamupatsa sopo. Adathirira mamuna wake mkala wa mchira wabuluzi m'mowa pamene mamunayo ankazemberana ndi Nanzunga. Adachita izi kuti mamuna wake, Ndileya, abwererenso kwa iye.

Chidazi

Atsibweni ake a Nadzonzi omwe adapereka umboni pabwalo lamilandu woti Nadzonzi amamenyedwa ndi mamuna wake.

Nachuma

Mchemwali wake wamkulu wa Nadzonzi yemwe adauza bwalo kuti Nadzonzi ndi yemwe adathira mkala wamchira wabuluzi m'mowa wa mamuna wake.

Amfumu

Adafufuza bwinobwino mlandu womwe Ndileya adasumira mkazi wake Nadzonzi ndipo adapereka chigamulo choyenera. Sadathetse banja la Ndileya ndi Nadzonzi monga amafunira Ndileya. Adapereka malangizo abwino kwa anthu onse awiriwa (Ndileya ndi Nadzonzi) nawauza kuti ayanjane.

Malo mwachidule

- a) Kunyumba kwa Ndileya ndi Nadzonzi
- b) Kuchitsime

- c) Kunyumba kwa Nasiwelo
- d) Ku Zomba (kuchipatala cha anthu amisala)
- e) Kunyumba kwa a Chidazi
- f) Ku bwalo lamilandu (kwa amfumu)

NUNSU YOYAMBA

Kunyumba kwa Ndileya

Ndileya akufika kumene kunyumba kuchokera kodula nsungwi adapeza mkazi wake Nadzonzi kulibe ali kuchitsime kotunga madzi. M'kudziyanhulira kwake, Ndileya adaulula kuti pakhomo sipanali bwino:

- a) Nkhuku zinali balala.
- b) Mbuzi zinali kunja pachingwe.
- c) M'nyumba munali mosasesa.
- d) Mabulangeti anali okuda kwambiri.

Makhalidwe a Nadzonzi

- a) Kumwa mowa
- b) Kuchita miseche
- c) Ulesi
- d) Kusamala zinthu ndi ana

Umboni woti Nadzonzi anali mlesi komanso mtchisi

- a) Adakhala zaka zitatu osachapa mabulangeti.
- b) Mamuna wake adampatsa sopo koma samachapa zovala.
- c) Chilundu chomwe adavala panthawiyi chinali nakanaka.
- d) Adakhala kwa mwezi wathunthu osasesa m'nyumba.
- e) Sadaphikire ana mpaka adachoka pakhomo.

Umboni woti Ndileya ankamumenya Nadzonzi

Pamene Nadzonzi adamuza Ndileya kuti adachedwa kuchitsime popeza chidayamba kuphwa mwakuti ankachita kudikira kuti madzi adzadze, Ndileya sadakhutire ndipo adamuza Nadzonzi kuti ichi ndi chifukwa chomwe adapeza. Nadzonzi adapepesa nati m'mene anamumenyera sabata yapitayo sanali kupeza bwino mwakuti sakadatha kuyenda mwachangu.

Kumbutso:

Ndileya adauza Nadzonzi kuti utchisi wake wamukwana ndipo m'kuyankhula kwake adasonyeza kuti ankalakalaka atapeza mkazi wina.

Zomwe zidasonyeza kuti Ndileya ankafunadi mkazi wina

- a) Adamuyerekeza mkazi wake ndi duwa lofota ndi dzuwa ndipo adamuza kuti ankafuna kaduwa katsopano kosiyana ndi Nadzonziyo.
- b) Adati mkazi watsopano akadatha kusamala m'nyumba ndi zinthu mwaukhondo.
- c) Adatsindika kuti adatopa ndi moyo wankhumba (wauve).
- d) Adanenanso kuti m'nyumba mwake mumafanana ndi m'khola poti munali mwanyansi: zinthu zinali mbwee.

Chipanda chamowa chidzetsa mkangano pakati pa Nadzonzi ndi mamuna wake Ndileya

- a) Ndileya adakayikira kuti Nadzonzi adamuyikiramo mankhwala m'chipandamo popeza chidagwa n'kusweka iye atangoyamba kumwa komanso mumaoneka tinthu takuda.



- b) Ndileya adafunsa Nadzonzi ngati sadamuyikire chiphe m'mowawo koma Nadzonzi adakanitsitsa.
- c) Nadzonzi adauza mamuna wakeyo kuti mowawo adapatsidwa ndi Nasiwelo. Ndileya adakwiya kwambiri ndi nkhanisi popeza Nasiwelo ankatchuka ndi mchitidwe wopeperetsa amuna okwatira.
- d) Ndileya adamuopseza mkazi wake Nadzonzi ndi mpeni mpaka adaulula kuti adamuyikira mankhwala m'mowawo. Iye adati adachita zimenezi kuti Ndileya abwerere kwa iye kuchoka Nanzunga, mkazi yemwe ankazemeberana naye ndipo ankakagona kunyumba kwake usiku uliwonse.

Kumbutso:

- Ndileya adayitanitsa Nachuma (mchemwali wake wamkulu wa Nadzonzi) kuti adzamve zomwe adachita mchemwali wake.
- Nachuma ataona kuti sayikwanitsa yekha nkhanisiyo, adapempha Ndileya kuti apite akawafotokozere atsibweni ake a Nadzonzi a Chidazi.
- Nadzonzi adayankhula kuti Ndileya anali ndi chikondi chabodza: analonjeza zomukonda Nadzonzi pachisoni ndi pachimwemwe koma panthawiyi anali kuzemberana ndi Nanzunga mwakuti sanali kumulabadiranso iye monga mkazi wake.

Zipangizo

1. Voko

Mtolo wansungwi uli panjapo wandiphadi.

2. Zining'a

- a) Pali kangauke pam'mero panga.
 - Ndili ndi chipemba kwambiri.
- b) Inetu sindipindira iwe manja anga.
 - Inetu sindigwirira iwe ntchito.
- c) Moyo wankumbawu
 - Moyo wauvewu/ moyo wautchisiwu
- d) Moti mutha kundigeya?
 - Moti mutha kundisiya banja?

Maphunziro m'gawoli

1. Utchisi

Nadzonzi:

- a) adakhala zaka zitatu osachapa mabulangeti.
- b) mamuna wake adampatsa sopo koma samachapa zovala.
- c) chilundu chomwe adavala panthawiyi chinali nakanaka.
- d) adakhala kwa mwezi wathunthu osasesa m'nyumba.

2. Zikhulupiriro

- a) Ndileya adakhulupirira kuti mkazi wapabanja akamacheza ndi mbeta ndiye kuti akukhalira miseche.
- b) Ndileya adakhulupirira kuti Nadzonzi anamuyikira mankhwala (mkala wamchira wabuluzi) m'mowa pamene chipanda chidagwa n'kusweka iye atangoyamba kumene kumwa mowa.

3. Kunyoza

- Ndileya ankamutcha Nadzonzi mlesi, chidzete komanso mtchisi.



4. Nkhanza

- Ndileya adamenya mkazi ndipo mkaziyo adavutikabe kwa masiku angapo kuti akwanitse kuyenda mwachangu.

NUNSU YACHIWIRI

Kunyumba kwa a Chidazi

Ndileya adafikako mwaukali akumunyoza Nadzonzi kuti ndi chidzete komanso adadumpha malire. Iye adauza a Chidazi kuti mdzukululu wawo adamuthirira mkala wamchira wabuluzi m'mowa.

Zotumphuka m'nunsuyi

- A Chidazi ankadziwa kuti Ndileya amamumenya mkazi wake.
- Ndileya sanali kuwawopa a Chidazi.

Matanthauzo a mawu

Chidzete : chitsiru

Wadumpha malire : waonjeza

NUNSU YACHITATU

Kunyumba kwa Ndileya

A Chidazi adziwa chilungamo

- Adafunsa mdzukululu wawo Nadzonzi kuti afotokoze chomwe chidamuchititsa kuti athirire mamuna wake mkala wamchira wabuluzi m'mowa.
- Poyamba Nadzonzi adanama kuti ndi Nasiwelo yemwe adamunyenga zoti athirire Ndileya mankhwala m'mowa.

c) Nadzonzi adauza atsibweni akewo kuti adamuthirira Ndileya mkala wamchira wabuluzi m'mowa popeza amafuna kuti abwerere kwa iye; achoke kwa Nanzunga komwe ankagona usiku uliwonse.

d) Nadzonzi adafotokozerana atsibweni akewo kuti mwezi udatha mamuna wake asakugona m'nyumb mwake koma ankakagona kwa Nanzunga ndipo Nasiwelo adamulangiza kuti atha kukhwimitsa chikondi chake ndi Ndileya mamuna wake pomupatsa mankhwala achikondi.

Pamfundozi a Chidazi adayankha zotsatirazi:

- Nasiwelo adamunamiza Nadzonzi (adamunyenga kudya nyama yagalu) mwakuti adakwiyitsa mamuna wake (adaponya muvi mumtima mwa mwamuna wake.)
- Nadzonzi akadawadziwitsa ndipo akadapeza njira yabwino yothetsera vutoli.

Pamene Ndileya adamva mawu a Nadzonzi (kuti iye adamupempha mankhwala Nasiwelo) adamuthamangitsa ndipo adamunyoza kuti ndi mdyerekezi komanso ndi wodetsedwa. Iye adati sadagwiritse ntchito mankhwala kuti Nadzonzi amulole.

Zotumphuka m'gawoli

- Akazi ndi ogona popeza amatsatira zilizonse zomwe amawanong'oneza anthu amene amati ndi anzawo; makamaka amene amasangalatsidwa ndi mjedo. (mawu a a Chidazi komanso Ndileya)

NUNSU YACHINAYI

Ku bwalo lamilandu

Mfumu idathokoza anthu kamba kobwera kumilandu m'malo mopita kukakolola.

Madandu a Ndileya pabwalo lamilandu

- a) Akuzunzika kwambiri ndi Nadzonzi.
- b) Nadzonzi sasasa m'nyumba (wakhala mwezi wathunthu osasasa m'nyumba)
- c) Nadzonzi sadalotche zipupa kuchokera tsiku lomwe adakwatirana.
- d) Nadzonzi sachapa zovala ngakhale amamugulira sopo.
- e) Nadzonzi saphikira ana.
- f) Nadzonzi amachoka pakhomo m'mawa nkumakabwera madzulo.
- g) Nadzonzi sasiya madzi panyumba/pakhomo.
- h) Nadzonzi adamuthirira mkala wamchira wabuluzi m'mowa.

Mawu a Nachuma, mboni ya Ndileya

- a) Adauza bwalo kuti padalibe aliyense pamene Nadzonzi ankapereka mowa kwa mamuna wake.
- b) Adavomereza kuti Nadzonzi adathirira mamuna wake mankhwala (mkala wamchira wabuluzi) m'mowa.
- c) Iye adauza bwalo kuti ngakhale iye kudalibe, koma Nadzonzi mwini wake adavomereza kuti adayika mankhwala m'mowa womwe adapereka kwa mamuna wake Ndileya.

- d) Adatsimikizira bwalo kuti mkala womwe unathiridwa m'mowa sunali mwaye popeza unali ndi mphumphu zazikuluzikulu kuposa mwaye.

Madandu a Nadzonzi

- a) Mamuna wake Ndileya amamumenya sabata iliyonse pofuna kumuchititsa kuti amusiye.
- b) Ndileya amafuna kukwatira Nanzunga; adamugulira nyama yang'ombe kambirimbi pamene iye ndi ana ake ankadyera mnkhwani.
- c) Akaphika nsima, Ndileya amangodya mwapatalipatali.
- d) Ndileya wakhala akugona kwa Nanzunga kwa sabata zambiri.
- e) Ndileya amamunyoza komanso amamukwiwira kawirikawiri.

Mawu a Chidazi mboni ya Nadzonzi

Adauza bwalo zinthu zotsatirazi:

- a) Ndileya ndi wankhanza komanso wautambwali.
- b) Ndileya amamumenya mkazi wake mwakuti mkaziyo wakhala akudandaula.
- c) Nadzonzi sadamuze zoti mamuna wake Ndileya akuyenda ndi Nanzunga.
- d) Nadzonzi akutayirira pankhani yogwira ntchito pakhomo monga kusesa m'nyumba popeza akukhumudwitsidwa ndi khalidwe la Ndileya.

Umboni woti Nadzonzi ankamenyedwa ndi mamuna wake Ndileya

- a) Mkono wake wamanja unali wosupuka.

- b) Anali ndi zipsera pachipumi chake.
- c) Anali ndi bala pamsana pake.

Mayankho a Ndileya kwa mfumu pankhani yomenya Nadzonzi komanso kuchita ubwenzi ndi Nanzunga

Adavomera nkhanizi ndipo adati:

- a) Nandzonzi ndi amene amamuchititsa kuti azimumenya.
- b) Nadzonzi ndi cholengedwa chopusa komanso chamtima wapachala (wosachedwa kukwiya).

Malangizo amfumu asanapereke chigamulo

- a) Kwa Nadzonzi
 - i. Aziuza atsibweni ake mamuna wake akamulakwira ndipo ngati sakuyanjana kwa atsibweni ake azikagwada kubwalo lamilandu.
 - ii. Sakuyenera kupereka yekha chigamulo monga adachitira pothirira mamuna wake mankhwala m'mowa.
 - iii. Asamagwiritse ntchito mankhwala pofuna kuti mamuna wake amukonde.
 - iv. Chikondi sagula, sakakamiza komanso sapanga ngati zidole.
 - v. Chikondi ndi mphatso yachilengedwe yochokera kwa Chiuta.
- b) Kwa Ndileya
 - i. Azidziwitsa atsibweni ake a mkazi wake ngati mkaziyo walkwitsa kanthu.
 - ii. Adachita zachibwana pozemberana ndi Nanzunga.

- iii. Akhale wokhulupirika kwa mkazi wake ndipo ndi wake mpaka muyaya.

Chigamulo chamfumu

- a) Sadapeze zifukwa zokwanira zothetsera banja la Ndileya ndi Nadzonzi.
- b) Ndileya ayanjane ndi mkaziw wake Nadzonzi.
- c) Nandzonzi apereke dipo la mbuzi kubwao la mfumu kamba kophwanya malamulo amudzi pomuthirira mankhwala (mkala wamchira wabuluzi) mamuna wake m'mowa.
- d) Ndileya salandira kanthu kuchokera kwa mkazi wake m'malo mwake abwerere kunyumba azikakhala naye.
- e) Ndileya azikumbukira kuti kumenya sikumasandutsa chinthu choyipa kukhala chabwino.

Zipangizo

1. Mkuluwiko

- **Wamva m'mimba ndiye atsekula chitseko.**
 - Amene ali ndi vuto ndi yemwe amasaka thandizo.

2. Zining'a

- a) **Bwalo ndilo liphwanye mutu wanyani**
 - Bwalo ndilo lipereke chigamulo kapena chilango.
- b) **Chamtima wapachala**
 - Chosachedwa kukwiya kapena kunyanyala
- c) **Ziphaliwali**
 - Ukali kapena kulalata
- d) **Igwa apa**
 - Lipira

Maphunziro

1. Nkhanza

- Ndileya ankamumenya mkazi wake Nadzonzi mwakuti adasupuka pamkono, adali ndi zipsera pachipumi komanso anali ndi bala kumsana. Kumenyedwaku kudachititsa Nadzonzi kuti akanike kuyenda mwachangu pochokera kuchitsime kotunga madzi.

2. Kupirira

- Ngakhale Nadzonzi ankachitidwa nkhanza ndi mamuna wake (kumumenya komanso kuzemberana ndi Nanzunga) iye sadathetse banja ndi mamuna wake Ndileya. Iye adauza bwalo kuti amamukondabe Ndileya.

3. Chilungamo

- Amfumu adagamula kuti Ndileya ayanjane ndi Nadzonzi mkazi wake ndipo kuti iwo sadapeze zifukwa zokwanira kuthetsa banja la anthu awiriwa.
- Nadzonzi adavomera kuti adathira mankhwala (mkala wamchira wabuluzi) m'mowa womwe adapereka kwa mamuna wake Ndileya ndipo adaonjeza kuti adachita zimenezi pofuna kuti Ndileya asiye kupita kwa Nanzunga, mkazi amene anali kuyenda naye ndipo adakhala akugona kwawo kwa sabata zambiri.
- Ndileya adamuza Nadzonzi kuti adatopa ndi utchisi komanso ulesi wake mwakuti anali kufuna

kukwatira mkazi wina yemwe angathe kusunga m'nyumba ndi katundu mwaukhondo.

- Nachuma adauza bwalo kuti padalibe munthu wina aliyense pamene Nadzonzi ankapereka mowa kwa mamuna wake Ndileya. Zoti anathira mkala wamchira wa buluzi m'mowa womwe adapereka kwa mamuna wake adadziwa popeza adawona mkalawo komanso mwini wakeyo, Nadzonzi adavomera kuti adathiramo mankhwalawo.
- Amalume ake a Nadzonzi, a Chidazi adauza bwalo kuti Ndileya amamumenya mkazi wake ndipo adaonetsa zipsera zomwe zinali pachipumi pa Nadzonzi, bala lomwe linali pamkono wake komanso kumsana kwake.

4. Banja si mankhwala

Mankhwala omwe Nadzonzi adakatenga kwa Nasiwelo nathirira Ndileya m'mowa kuti Ndileyayo achoke kwa Nanzunga n'kubwerera kwa iye sadagwire ntchito m'malo; mwake Ndileya adakasuma kubwalo lamilandu kwa amfumu kupempha kuti amusiye Nadzonzi.

Mawu ena ofunika kuwawunikira

1. Umanena chatsitsa dzaye kuti njovu ithyoke mnyanga

- a) Nadzonzi anali mtchisi komanso mlesi. Sankachapa zovala ndi mabulangete ngakhale mamuna wake Ndileya ankamugulira sopo. M'nyumba mumatha mwezi wathunthu mosasesedwa. Utchisi komanso ulesi umenewu ndi omwe udachititsa kuti Ndileya ayambe kuyenda ndi Nanzunga ndipo adakhulupirira

kuti mkazi watsopanoyu angathe kusamala m'nyumba komanso zinthu mwaukhondo. Pamene Ndileya adayamba kuyenda ndi Nanzunga, amachoka kunyumba usiku uliwonse nkumakagona kwa Nanzungayo ndipo adasiya kumulabadira mkazi wake Nadzonzi pamodzi ndi ana ake omwe.

- b) Mayendedwe a Ndileya ndi omwe adachititsa Nadzonzi kuti asakesake mankhwala (mkala wamchira wabuluzi) n'kumuthirira mamuna wakeyo m'mowa. Ngakhale Nadzonzi anali wautchisi ndi waulesi, ankamukonda Ndileya. Pamene Ndileya adayamba kuzemberana ndi Nanzunga, adasiya kumulabadira mkazi wake Nadzonzi. Akaphika nsima, Ndileya amangodya patalipatali. Amamugulira Nanzunga nyama yang'ombe pamene Nadzonzi ndi ana ake anali kudyera mnkhwani. Kwa sabata zochuluka Ndileya ankagona kwa Nanzunga. Pachifukwachi, Nadzonzi adamuthirira mankhwala m'mowa olimbikitsa chikondi kuti achoke kwa Nanzunga n'kubwerera kwa iye monga kale.

2. Kulephera udindo

- a) Atsibweni ake a Nachuma ndi Nadzonzi, a Chidazi, ankadziwa ndipo anali ndi umboni woti Ndileya ankamuchitira nkhanza mdzukululu wawo Nadzonzi koma palibe chomwe adachitapo monga kukasuma kubwalo lamilandu. M'malo mwake adakapereka umboniwu pamene Ndileya adakadandaula kubwalo

lamfumu kuti akufuna kumusiya banja Nadzonzi ndipo akufuna kukwatira mkazi wina.

- b) A Chidazi adakanika kuganiza mwakuya kuti aweruze nkhanzi ya mdzukululu wawo Nadzonzi ndi mamuna wake Ndileya. Iwo adangokhulupirira kuti Nadzonzi adalakwa koma sadafune kuunika bwinobwino chomwe chidachititsa Nadzonzi kuti amuyikire Ndileya mankhwala m'mowa. Adayankhula kuti akazi ndi ogona popeza amatsatira zilizonse zomwe amanong'onezedwa ndi anthu omwe amati ndi anzawo. Bambowa adakanika kumuuza Ndileya kuti nayenso anali olakwa m'malo mwake adauza Ndileya kuti iwo amusunga Nadzonzi mpaka tsiku lamilandu.
- c) Nadzonzi amakanika kuwaphikira ana asanachoke pakhomo. Monga mkazi wapabanja komanso mayi wa ana, Nadzonzi anayenera kuonetsetsa kuti ana adya asanapite kosewera komanso anayenera kudziwa komwe ana ake akupita. Ana a Nadzonzi adachoka osadya popita kukacheza ndipo amayi awo samadziwa komwe adalowera mpaka dzuwa lidalowa.

3. Zivumbulutso

Zinthu zomwe zidachititsa kuti zinthu zina zobisika zibwere poyera.

a) Kugwa ndi kusweka kwa chipanda chamowa

- Kupulumuka m'manja kwa chipangizochi, Ndileya atangoyamba kumwa mowa, komanso kusweka kwake kudachititsa kuti Ndileya akayikire zoti Nadzonzi adamuyikira mankhwala m'mowa.



Kusweka kwa chipangizochi kudachititsa kuti mkala wamchira wabuluzi womwe Nadzonzi adathira m'mowa uwoneke ndipo Ndileya adakwiya kwambiri.

b) Mpeni

- Chipangizochi chidathandizira kuti chilungamo chidziwike. Ndileya atamufunsa Nadzonzi kuti awulule yemwe adathira mankhwala m'mowa, iye adakanitsitsa kuti sakudziwa. Pamene Ndileya adatenga mpeni n'kumuza mkazi wakeyu kuti amupha nawo akapanda kuwulula yemwe anathira mankhwala m'mowa, iye (Nadzonzi) adawulula kuti adathira ndi iyeyo

c) Kupempha chisudzulo

- Kupempha chisudzulo kudachititsa kuti nkhanza za Ndileya zidziwike kubwalo lamilandu. Pamene Ndileya adayala madandaulo ake kubwalo lamilandu n'kupempha kuti amusiye Nadzonzi makamaka chifukwa adamuthirira mankhwala m'mowa, Nadzonzi adaulula kuti adamuthirira mankhwala achikondi popeza ankayenda ndi mkazi wina, sankagona pakomo komanso samamusamala pamodzi ndi ana ake omwe. Nadzonzi adaululanso kuti Ndileya amamumenya sabata iliyonse. Mboni ya Nadzonzi idanetsa mkono wosupuka wa Nadzonzi, zipsera pachipumi pake komanso bala kumsana kwake. Kusumaku kudaululitsanso kuti Ndileya adamugulira

Nanzunga nyama yang'ombe kambirimbi pamene iye ndi ana ake ankadyera nkhwani. Bwalo lidadziwanso za utchisi ndi ulesi wa Nadzonzi.

d) Mtsiriko womwe Ndileya adapatsidwa ndi malemu bambo ake

- Mtsiriko umenewu udathandizira kuti Ndileya adabwe ndipo azindikire kuti china chake chinayikidwa m'mowa womwe adapatsidwa kuti amwe.

MUTU 4

ZIKANI

(Smith Likongwe)

Ochita chisudzo

Mgezenge

Munthu wolemera wazaka makumi asanu ndi limodzi amene ankamuchitira nkhanza mkazi wake. Ankafuna ulemu wambiri kuchokera kwa mkazi wake komanso ankamusirira mlamu wake Zikani. Adachotsa wantchito wogulitsa mugolosa yake pazifukwa zosakwanira. Ankavutika ndi miyendo kamba ka ukalamba.

Nagama

Mkazi wa Mgezenge wazaka makumi anayi yemwe ankadwala kwambiri mwakuti ankakanika kugwira ntchito zina pakomo. Patapita adamwalira.

Gama ndi Abiti

Makolo a Nagama ndi Zikani omwe anali amphawi.

Anali adyera ndi ndalama. Adatengeka ndi ndalama za Mgezenge mwakuti pamene Nagama ankadwala adalolera zochita shazi kuti apitirize kulandila ndalama kuchokera kwa Mgezengeyo.

Zikani

Mwana wa a Gama yemwe ankasiriridwa ndi Mgezenge. Nangama ankamukhulupirira ndipo adamuza zina mwa zinthu zoyipa zomwe zimamuchitikira panyumba pake.

Chisomo

Mnzake wa Zikani yemwe adakakhala naye atathawa kubanja lokakamizidwa kuti akapitiriza sukulu.

Funsani

Mnyamata wogulitsa m'golosale ya Mgezenge yemwe adachotsedwa ntchito pazifukwa zosakwanira. Adathandizidwa ndi azungu amishoni mpaka adakafika ku yunivesite. Adakwatira Zikani.

Mayamiko

Mnyamata wachichepere yemwe adatumidwa ndi atate ake kuti akatule nkhu kwa Mgezenge.

Mfumu

Mfumu ya m'mudzi

Kamwendo

Tenanti (wogwira ntchito) pa esiteti yemwe sankazindikira kuti zomwe ankawachitira ana ake, monga kuwajombetsa kusukulu komanso kuwagwiritsa ntchito zopitirira msinkhu

wawo, zinali nkhanza. Adathamangitsa Zikani ndi Chisomo pamene ankamuunikira za ntchito zoyipitsitsa zomwe zimaononga tsogolo la ana.

Malo mwachidule

- a) Kunyumba kwa Mgezenge ndi Nagama
- b) Kunyumba kwa makolo a Zikani
- c) Kunkhalango komwe ankakhala Zikani ndi Chisomo
- d) Kusukulu
- e) Ku esiteti
- f) Kunyumba kwa Zikani ndi Funsani
- g) Kugolosale ya Mgezenge
- h) Kunyumba kwa a Kamwendo
- i) Mudzi woyandikana ndi nkhalango

NUNSU YOYAMBA

Mgezenge ndi Nagama kunyumba kwawo

Mgezenge akudziyankhulira yekha ndipo adandaula zinthu izi:

- a) Miyendo inkamuphwanya ndipo inkatero kamba kakuti iye adakalamba.
- b) Miyendo yake imafunika kukhala m'mwamba.
- c) Akazi ena akamakula amavuta kwambiri. (Adayankhula izi popeza mkazi wake Nagama adachedwetsa kubweretsa mpando woti apachikepo miyendo.)

Madandaulo a Mgezenge pamene amakambirana ndi mkazi wake

- a) Mkazi wake, Nagama, adachedwetsa mpando woti ayikepo miyendo.
- b) Iye ankadwala kusowa chisamaliro.
- c) Kusowa chikondi ndi chisamaliro ndi matenda ndithu.
- d) Ulemu wochokera kwa mkazi wake umaperewera. (Amamutchula “amuna anga” m’ malo mwa dzina lake “Mgezenge” pomuyitana ngakhale amalidziwa bwino dzinali.)
- e) Mkazi wakeyo amamuyankhula ali chilili.

Madandaulo a Nagama mkazi wa Mgezenge

- a) Adakumbutsa mamuna wake kuti iye anali kudwala mwakuti sankachitira dala kuchedwetsa kampando kopachikapo miyendo.
- b) Mgezenge, mamuna wake, sankamulabadira.
- c) Kumutchula mamuna wake “Mgezenge” si ulemu

Zotumphuka pa zokambirana za Mgezenge ndi mkazi wake

- a) Mgezenge ankamuyankhula mkazi wake moopseza komanso mwaukali.
- b) Mgezenge ankanyinyirika ndi kudwala kwa mkazi wake mwakuti adamuopseza kuti akwatira mkazi wina popeza iye (mkaziyo) sanali kugwira ntchito zambiri.
- c) Ku mayiko ena monga ku Nepal, Tibet, Sri Lanka ndi mbali zina za China, mkazi amatha kukwatiwa ndi amuna angapo. Mitala yochita mkaziyi imatchedwa *Poliyandire*.
- d) Banja la Mgezenge linali ndi zifuyo zambiri: ng’ombe zopitirira makumi asanu ndi awiri (70) komanso mbuzi

zana limodzi ndi makumi awiri kudza mphambu zisanu ndi zinayi (129).

Umboni woti pamafunika munthu wothandiza ntchito pakhomo pa mgezenge

- a) Zifuyo zinalibe mbusa choncho zinkaononga m’ minda ya wanthu.
- b) Zifuyo zimafunika munthu woti apite nazo ku dipi.
- c) Golosale imafunika dongosolo labwino.

Kumbutso

- a) Ngakhale pamafunika munthu woti athandize kugwira ntchito, monga kusamala ziweto pakhomo pa Mgezenge, yankho la vutoli silinali kukwatira mkazi wina monga amanenera Mgezenge.
- b) Pamene Nagama adauza mamuna wake Mgezenge kuti anali kuyankhula m’ zining’a, Mgezengoyo adalusa nakunga chibakera n’ kumuponyera mkazi wakeyo koma iye adzinda mwakuti Mgezenge adagwa pansi ndipo amaoneka kuti ankamva ululu kwambiri.

Mgezenge ndi Zikani

- a) Zikani adaulukira naodira kunyumba kwa Mgezenge panthawi yomwe Nagama adazinda chibakera cha Mgezenge kachiwiri ndipo Mgezenge adagwa ngati chithumba.
- b) Zikani adathandiza Mgezenge kuti adzuki ndipo Mgezenge adamukumbatira mosonyeza chikondi. Izi zidachititsa Zikani kuti amukankhe Mgezenge ndipo adatsala pang’ono kugwanso.

c) Zikani atawafunsa alamu ake a Mgezenge kuti afotokoze chomwe chinachitika kuti apezake atagwa, Mgezenge adamuyankha kuti adaterereka pamene ankafuna kuti akhale pampando.

Mgezenge asirira momufuna Zikani

Pamene Zikani adatsanzika nayamba kuyenda kuti alondole mkulu wake Nagama kukhitchini, Mgezenge adadziyankhulira mawu otsatirawa akumuyang'ana:

“Mulungu sungamumvetse. Adalenga munthu wamkazi kuti akhale wothangatira mamuna. Atamulenga mkaziyo, anapitiriza ndipo akupitiriza kumukongoletsa munthu wamkazi. Atsikana akubadwa masiku ano akuposa amawo kukongola. Ndipo Mulungu amati akalenga mwana wamkazi chaka chino, chaka chamawa amadzilenga njole yozunguza mutu. Atsikana amakono akamayenda amakhala ngati akuvina ndipo akamayankhula amakhala ngati akuimba nyimbo zanthetemya.”

Zotumphuka pa mkumano wa Mgezenge ndi Mayamiko

- a) Mayamiko adali mwana wa a Mackson Chikoya ndipo anali ndi zaka khumi ndi ziwiri (12).
- b) Mgezenge adagwirizana ndi bambo a Mayamiko kuti awapititsire nkuni koma mtengo weniweni ndi kuchuluka kwa nkuni (kukula kwa mtolo) sadagwirizane. Mayamiko adadziwa kuti mtolowo wakwanira pamene bambo ake adavomera ndi mutu pamene iye ankadutsa panyumba akupita kwa Mgezenge.
- c) Mayamiko ankachita malonda amakala.

d) Mayamiko sadapite kusukulu popeza atate ake adamujombetsa kuti akasake nkuni zomwe adakapereka kwa Mgezenge komanso zovala zake zinali zokuda mwakuti ankayembekezera kuti Mgezenge akampatsa ndalama zankuni zomwe adapititsazo, akagule sopo wochapira pobwerera kwawo.

e) Golosale ya Mgezenge idali yotseka ndipo Mgezenge adapsa mtima nati amuchotsa ntchito Funsani, mnyamata yemwe amagulitsa m'golosaleyi.

f) Mgezenge amamukhulupirira Funsani.

Zipangizo m'gawoli

1. Zifanifani

- a) Kumangoti amuna anga amuna anga muli pholi ngati mlongoti.
- b) Agwanso ngati chithumba.
- c) Osamathamangira kufunsa mafunso ngati aphunzitsi.
- d) Atsikana amakono akamayenda amakhala ngati akuvina
- e) Akamayankhula amakhala ngati akuimba nyimbo zanthetemya.”

2. Msemphano

- a) Zikani atawafunsa alamu ake a Mgezenge kuti afotokoze chomwe chinachitika kuti apezake atagwa, Mgezenge adamuyankha kuti adaterereka pamene ankafuna kuti akhale pampando. Zoonza zake n'zakuti Mgezenge adagwa pamene mkazi wake Nagama adazinda chibakera chomwe adamuponyera.

3. Mvekero

- pholi: chiimirire

Maphunziro m'nunsuyi

a) Bodza

- Zikani atawafunsa alamu ake a Mgezenge kuti afotokeze chomwe chinachitika kuti apezake atagwa, Mgezenge adamuyankha kuti adaterereka pamene ankafuna kuti akhale pampando.

b) Kusirira

- Mgezenge ankamusirira kwambiri mlamu wake Zikani mwakuti pamene ankamudzutsa, atagwa pamene Nagama adazinda chibakera chomwe adamuponyera, adamukumbatira mosonyeza chikondi.

c) Kuyipa kwa kuononga chilengedwe

- M'mudzi m'mene ankakhala Mgezenge ndi anthu ena mitengo idatha ndipo idayamba kusowa kamba ka m'chitidwe wootcha ndi kugulitsa makala.

d) Nkhanza

- Mgezenge adafuna kumenya mkazi wake pazifukwa zosakwanira.

e) Kukhulipirira wantchito

- Mgezenge adamusiyira Funsani makiyi akugolosale.

f) Kumvera makolo

- Bambo Chikoya adamujombetsa mwana wawo Mayamiko kuti akasake nkhuhi ndipo akazitule kwa

Mgezenge. Mayamiko adajombadi nachita zomwe adauzidwa ndi atate ake.

g) Kuganiza mosiyana

- Nagama ankamuyitana mamuna wake Mgezenge pomutchula kuti “amuna anga” ndipo adaona kuti ankachita ulemu poteropo. Mgezenge sankasangalatsidwa ndi mchitidwewu ndipo adauza mkazi wakeyo kuti ndi mwano kuti azimutchula “amuna anga” chonsecho dzina lake anali kulidziwa.

NUNSU YACHIWIRI

Zotumphuka pamacheza a Nagama ndi Zikani

- Nagama adadabwa kuti Zikani adafika kunyumba kwake panthawi yomwe anayenera kupezeka m'kalasi kusukulu.
- Zikani adathangitsidwa kusukulu popeza sadapereke ndalama zochitira chitukuko pasukulu (monga kumanga zimbudzi) komanso zogulira bukhu lomwe adataya.
- Bukhu lomwe Zikani anayenera kulipira lidasowa pamene iye adapita kukadzithandiza kuchimbudzi.
- Pasukulu pomwe Zikani ankaphunzira pamafunikadi zimbudzi zoonjezera popeza ophunzira ankakhala pamzere wautali nkumadikirana kuti alowe ku zimbudzi zomwe zinalipo.
- Nagama adandaula zinthu zotsatirazi malingana ndi kubedwa kwa bukhu la Zikani:
 - Kuba ndi koipa m'dziko popeza kumachititsa kuti mwini katundu avutike.

- ii. Anthu amene amakhala akuba pasukulu sasiya mwansanga.
 - iii. Anthu amene akuba makonowa adayamba m'chitidwewu adakali ana.
- f) Makolo a Zikani ankadalira banja la Nagama pankhani zachuma.
 - g) Mkazi akalowa m'banja kamba ka umphawi, amakhalira kumulambira mamunayo.
 - h) Mgezenge akakwiya ndi chinthu, mkwiyo umathera pa mkazi wake Nagama.
 - i) Nagama amakhala mwamantha ndi mamuna wake koma ankamumasukira mchemwali wake Zikani.

Maphunziro m'nunsuyi

a) Kuba ndi koipa m'dziko popeza kumachititsa kuti mwini katundu avutike.

Wophunzira wina adaba bukhu la Zikani kotero kuti Zikani anayenera kulipira.

b) Kudalira

- Zikani adadalira makolo ake kuti amupatsa ndalama zochitira chitukuko pasukulu komanso zolipirira bukhu lomwe adataya.
- Makolo a Zikani ankadalira kwambiri banja la Mgezenge ndi Nagama pankhani zachuma.
- Zikani adadalira mnzake kuti amuyang'anira bukhu pamene iye adapita kukadzithandiza.

c) Nkhanza

- Mgezenge chilichonse chikamuvuta, mkwiyo umadzathera pa mkazi wake.

Zipangizo

1. Mikuluwiko

a) Wamva m'mimba ndiye atsekula kukhomo.

- Amene ali ndi vuto ndipo akufuna chithandizo mwansanga, akuyenera kuchitapo kanthu.

b) Wopempha safulumira.

- Wopempha amayendera maganizo a wopereka chithandizoyo.

2. Msemphano

- Azimayi am'mudzi ankachitira nsanje Nagama ponena kuti adakwatiwa ndi mamuna wolemera (adakwa kwa n'kumbuyo komwe). Azimayiwa sankadziwa kuti Mgezenge anali mamuna wovuta mwakuti Nagama ankavutika ndipo amakhala moyo womulambira. Chilichonse chikamuvuta, mkwiyo umadzathera pa mkazi wake.

NUNSU YACHITATU

Mgezenge ndi Funsani ku golosale

- a) Mgezenge adakwiya kwambiri popeza Funsani sanatsekule golosale ndipo pamene adatulukira adamutchula kuti ndi wopusa.
- b) Funsani sadatsekule golosale chifukwa ankadwala ndipo adapita kukalandira thandizo lamankhwala kuchipatala.

Mgezenge sadamve izi: adangoti Funsani ndi wopusa komanso waulesi.

- c) Mgezenge adauza Funsani kuti achite sitoko patsikulo ngakhale kuti Funsaniyo sankadziwa tanthauzo lake.
- d) Mgezenge adayankhula kuti makolo a Funsani ankagwira ntchito pa esiteti ya Mgezenge koma adapititsidwa ku esiteti ya mnzake wa Mgezenge kutali. Pochoka iwo adavomereza kuti Funsani atsale azigwira ntchito mgolosale ya Mgezenge.
- e) Ngakhale Funsani adamuza Mgezenge kuti cholemba chomwe adachiyeza m'tumba mwake adachita kugula kuti azilemba, Mgezenge sadamumvere ndipo adamuchotsa ntchito namuza kuti malipiro ake ndi cholemba chomwe adatengacho.

Maphunziro m'nunsuyi

1. Nkhanza

Mgezenge:

- a) Adamulemba ntchito Funsani ngakhale adali mwana wazaka khumi ndi ziwiri (12).
- b) Adamunyoza Funsani pamene sadatsegule golosale kamba kotu adapita kuchipatala kukalandira thandizo lamankhwala pamene adadwala malungo.
- c) Adachotsa ntchito Funsani popanda zifukwa zokwanira.
- d) Adamukwenya pakhosi Funsani ndipo sadampatse malipiro pamene adamuchotsa ntchito ponena kuti malipiro ake ndi cholemba chomwe chidapezeka m'tumba lake.

2. Kukayikira/Kuganiza molakwika

- Mgezenge adauza Funsani kuti makolo ake povomereza zomusiya kuti azigwira ntchito mugolosale ya Mgezenge adagwirizana zoti amubere.

3. Umphawi umachititsa munthu kuti aganize moperewera.

Makolo a Funsani adavomereza zomusiya mwana wawo wazaka khumi ndi ziwiri kuti azigwira ntchito m'golosale ya Mgezenge pamene iwo amatumizidwa kukagwira ntchito kutali ku esiteti ya mnzake wa Mgezenge zotsatira zake Mgezenge adamuchita nkhanza mwanayo.

Zipangizo

1. Zining'a

a) Malungo adandithyola mafupa.

- Malungo anandivuta zedi./Ndinadwala malungo kwambiri

b) Ndipsi

- wakuba

Matanthauzo a mawu

Sitoko: Kuwerengera katundu yemwe watsala m'shopu pofuna kupeza katundu amene watuluka ndi kufananitsa ndi ndalama zomwe zilipo katunduyo atagulitsidwa.

NUNSU YACHINAYI

Zotumphuka pa kucheza kwa Abiti ndi Gama

Kunyumba kwawo pambuyo pa msonkhano wa kwa

Agulupu



- a) Monga Mgezenge, naye Gama anali wosachedwa kupsa mtima ndipo mkazi akamamuyankhula ali chilili amatanthauzira kuti ndi mwano. (Mkazi wake, Abiti, atayankha kuti si amfumu amene adapereka chigamulo cha nkhani yamunda iye adapinda chibakera namuloza nacho nkumuuzanso kuti safuna zopusa.)
- b) Chitukuko chamsewu ndi chomwe chidautsa mapiri pachigwa.
- c) Amfumu (Agulupu Watison Kajiyanike Jere) adauza Gama kuti msewu udutsa m'munda mwake ndipo "road reserve boundary" imadyanso gawo lalikulu zedi lamundawo.
- d) A Gulupu Watison Kajiyanike Jere ankaopedwa m'mudzi kamba ka zamatsenga zomwe adamuchita mlamu wawo (atawalakwira nkukana kupepesa, adangomutchula dzina ndipo iye adachita khungu ali kutauni).
- e) Anthu m'mudzimu adaononga mitengo ndi malonda amakala.
- f) Agulupu adayankhulam anthu mwamwano komabe adayankhula chilungamo.

Mgezenge akamutula Nagama kwa makolo ake

- a) Adatulukira atomugwira padzanja ndipo adayankhula mwamwano ndi makolo a Nagamayo kuti akudzamusiya koma a Gama adamuyankha mwaukali namuuzza kuti akhale pansi popeza sakadagona usiku ngati sakadathana naye masana atsikulo.

- b) Nagama adandaula kuti Mgezenge adamumenya usiku wonse.
- c) Mgezenge adapereka dandaulo lake kudzera m'zing'ana ziwiri: mpando ndi mbalame. (Munthu amene ali ndi mpando koma nkumagona pansi, mutu wake ndi wosakoka. Mbalame yomwe ili ndi chisa koma ikuopa kugona poti muli njoka, singalimbe mtima kuti ilowemo m'chisamo.) Apa Mgezenge amafuna kutanthauza kuti sakukhala pamodzi ndi mkazi wake monga banja kamba ka zovuta zina zomwe kwa iye zinali zosakwanira.

Zotumphuka pazokambiranazi

- a) Mgezenge ndi Gama anali amuna osachedwa kupsa mtima.
- b) Mkazi wa Gama, Abiti, amatsatira nkhani ndipo amamvetsa zinthu.
- c) Abiti ndi mamuna wake Gama anakomedwa ndi chuma cha Mgezenge mwakuti sanali kukonza mavuto a banja la mwana wawo Nagama moyenera. Iwo amalimbikira kumuuzza Nagama kuti sakufuna kuti awathawitsire mkamwini wabwinobwinoyo.
- d) Mgezenge ankamufuna kwambiri Zikani.
- e) Abiti ndi mamuna wake anali wokonzeka kumupereka mwana wawo Zikani kwa Mgezenge kuti akhale mkazi wake wachiwiri n'cholinga choti apitirize kulandira ndalama zake.

Zomwe zidachititsa Makolo a Nagama kuti achite Shazi/Mbirigha/Isakulwa/Nthena

- a) Nagama adakhala pafupifupi chaka chathunthu asakupeza bwino mwakuti Mgezenge sanali kulowa m'nyumba.
- b) Samafuna kuti Mgezenge ayambe kuzemberana ndi akazi adera.

Matenda a Nagama

- Amatsegula m'mimba, ankangomva thupi kuphwanya komanso amadwala malungo pafupipafupi.

Umboni woti Abiti ndi Gama amafuna Mgezenge akwatirensa Zikani popeza Iwo adali ndi dyera pa chuma cha Mgezenge.

Pamene Mgezenge adadzamutula Nagama kunyumba kwawo, makolowa adamuza Nagama zinthu zotsatirazi:

- a) Munthu akaweta galu amayenera kumupatsa chakudya zonse chifukwa akapanda kutero amagwira nkuku za eni.
- b) Mlimi wang'ombe yamkaka amayenera kuyipatsa msipu ndi chakudya china choyenera ngati akufuna izimupatsa mkaka wambiri ndipo ayenera kuonetsetsa kuti ng'ombeyo sikuchoka m'khola.
- c) Akatswiri ankhondo amene amadumpha m'ndege yatombolombo; amene amadumpha ndi chipangizo chokhala ngati chiambulera sangabwerere m'ndege adadumphamo kale.
- d) Adamuza Zikani kuti akufuna kuchita mwambo wa "Shazi" ndipo adamufotokoza momveka bwino zifukwa zomwe iwo amafunira kuchita mwambowo.

Zipangizo

1. Zifanifani

- Mukungoberekana ngati makoswe:
 - ✓ Mukuberekana kwambiri

2. Zining'a

- a) Chiunda (kankhunda kakang'ono)
 - ✓ Zikani
- b) Nkhunda yayikulu
 - ✓ Nagama, mkazi wa Mgezenge
- c) Akuthandize kusenya mtolo
 - ✓ Azigona ndi mamuna wako kuti aleke kudandaula
- d) Mwamuna azingoyang'ana kudenga
 - ✓ Azingokhala osagona ndi mkazi wake.
- e) Mgodu
 - ✓ Popezera ndalama ndi thandizo lina lofunikira
- f) Kuwedza chambo chonona kenako n'kuchitayira m'madzi momwemo
 - ✓ Kupeza mamuna wachuma ndi kumusiyanaso
- g) Sakulowa m'nyumba
 - ✓ Sakugona ndi mkazi wake monga banja.
- h) Kutaya bomwetamweta
 - ✓ Kutaya mamuna wopezapeza
- i) Zidzete
 - ✓ Zitsiru/Opusa/Opepera

3. Mikuluwiko

- a) Zengerezu adalinda kwawukwawu.
 - ✓ Chidodo chimabweretsa mavuto.

b) Munthu akaweta galu amayenera kumupatsa zakudya nthawi zonse chifukwa akapanda kutero amagwira nkukhuku za eni.

✓ Mgezenge, pamene adakwatira Nagama, anayenera kupatsidwanso Zikani ngati Nagamayo samakwanitsa zinthu zoyenera m'banjamo poopetsa kuti angatenge mkazi wadera osati m'bale wake wa Nagamayo.

c) Mlimi wang'ombe yamkaka amayenera kuyipatsa msipu ndi chakudya china choyenera ngati akufuna izimupatsa mkaka wambiri ndipo ayenera kuonetsetsa kuti ng'ombeyo sikuchoka m'khola.

✓ Kuti Mgezenge apitirize kupereka ndalama zambiri kwa apongozi ake, apongoziwo anayenera kumupatsanso Zikani ngati mkazi wabasera/wabanyira.

d) Akatswiri ankhondo amene amadumpha m'ndege yatombolombo; amene amadumpha ndi chipangizo chokhala ngati chiambulera sangabwerere m'ndege adadumphamo kale.

✓ Makolo a Zikani adachita chisankho chochita mwambo wa 'Shazi' mwakuti sakadathanso kubwerera m'mbuyo n'kusintha maganizo kamba ka maganizo a Zikaniyo.

Maphunziro m'nunsuyi

1. Mwano

➤ A gulupu adayankhula mwamwano kuti iwo sangakulitse dziko, pamene anthu ankawadandaulira

kuti asowa malom olima malingana ndi kubwera kwa msewu.

2. Ndalama ikayankhula, chilungamo chimakhala chete.

➤ Mgezenge amapereka ndalama zambiri kwa apongozi ake ndipo patsiku limene adapita ndi madandaulo ake nkukamusiya Nagama, adatenganso ndalama zambiri nawapatsa amayi ake. Ndalama zimenezi zidachititsa kuti makolo asaganizire bwino mavuto omwe mwana wawo amakumana nawo kubanja. Iwo adaganiza zopereka Zikani, mng'ono wake wa Nagama kwa Mgezenge kuti akhale mkazi wake wachiwiri n'cholinga choti azilandirabe ndalama. Makolowa amadziwa ndithu kuti Zikani ndi mlamu wake wa Mgezenge koma adamuperekabe kamba ka ndalama.

3. Nkhanza

a) Makolo a Zikani adamusiyitsa sukulu mtsikanayu kuti akwatiwe ndi mlamu wake Mgezenge.

b) Mayi a Nagama adamuza kuti alibe mphamvu zowatsutsa pamene iwo ankamuza za ganizo loti Zikani alowe m'nyumba mwake ngati mkazi wachiwiri wa Mgezenge.

c) Mgezenge amafuna adzilowa m'nyumba ngakhale mkazi wake anali akudwala.

4. Dyera

➤ Abiti adauza Nagama kuti sankafuna zoti Mgezenge akwatire kwina; akhalebe m'banja lawo kuti ateteze chuma. Adamulangizanso kuti iwo adayiyambitsa



nkhaniyi popeza adaona kuti mwana wawoyo akufuna kutaya bomwetamweta. Iwo adamulangiza zochita 'Shazi' kuti mamuna asamuthawe.

5. Ufulu

- Zikani adauza bambo ake kuti anali ndi ufulu wopitiriza maphunziro mwakuti atate akewo sangamukakamize zokalowa m'nyumba mwa Mgezenge mlamu wake ngati mkazi wake wachiwiri.

6. Kusamva maganizo a ena

- Makolo a Zikani sadafune kumva maganizo a mwana wawo pamene ankamupereka ngati shazi kwa Mgezenge. Kuonjezera apo, a Gama adatsindika pomuuza Zikani kuti zimene iwo alamula, alamula basi; palibe alandulepo.

Matanthauzo amawu

Shazi/Mbirigha/Isakulwa/ Nthena:

- Mkazi wabasera/wabanyira (woonjezera kwa mamuna) pomuthokoza mamunayo kamba ka mtima wake wabwino kapena wothandiza. Chifukwa china chimakhala choti mkazi wachiwiriyo abereke ana pamene mkazi woyamba akukanika.

NUNSU YACHISANU

Mgezenge akwatira Zikani

Mwambo udayamba mwachilendo ndi kuyankhula kwa makolo akuchikazi.

Mawu a Gama, bambo a Zikani

- a) Zikani adamutuma zoti anene kuti iye adasangalala polowa m'banja ndipo ndi amene adapereka ganizo loti achite shazi.
- b) Ukwati wa Zikani ndi Mgezenge udalimbitsa ubale womwe udalipo kale.(Adakhala ngati nyumba yanjerwa yomwe akuyipaka pulasitala wasimenti.)
- c) Adayamika mkamwini wake Mgezenge kamba ka thandizo lomwe amapereka komanso kamba ng'ombe ziwiri zomwe adapha patsikuli zomwe nyama yake anthu ankakanika kuyitsiriza.

Kumbutso

Akuchimuna sadayankhule popeza padalibepo komanso padalibe yemwe adawayimirira.

Zipangizo

Msemphano

- Gama adauza anthu kuti Zikani adamutuma kuti anene kuti iye wakondwa polowa m'banja komanso adaonjeza kuti Zikani ndi yemwe adapereka ganizo loti achite mwambo wa shazi chonsecho Zikani sadapereke ganizoli ndipo sadakondwere nkomwe polowa m'banja.

Maphunziro

1. Bodza

- Gama adauza anthu kuti Zikani adamutuma kuti anene kuti iye wakondwa polowa m'banja komanso adaonjeza kuti Zikani ndi yemwe adapereka ganizo loti achite mwambo wa shazi chonsecho Zikani

sadapereke ganizoli ndipo sadakondwere nkomwe polowa m'banja.

2. Zinthu zosalongosoka

- Pamene Zikani amalowa m'banja ndi Mgezenge monga banja lachiwiri, akuchikazi padalibe komanso padalibe yemwe adawayimirira mwakuti sadayankhulepo.

NUNSU YACHISANU NDI CHIMODZI

Mkangano kunyumba kwa Mgezenge pambuyo pa ukwati

Mkangano woyamba udali pakati pa Mgezenge ndi Nagama.

- a) Mgezenge adauza Nagama kuti akatulutse katundu wake kuchipinda chachikulu chomwe amagona ndipo akalowe kuchipinda cha alendo kuti apereke danga kwa Zikani.
- b) Nagama adauza Mgezenge kuti iye ndi amene atasamukire kuchipinda chomwe azikagona ndi Zikani.
- c) Mokwiya, Nagama adatulutsa katundu wake kuchipinda chachikulu nasiya Mgezenge ndi Zikani.

Mkangano wachiwiri unali pakati pa Mgezenge ndi Zikani. Atatuluka Nagama zinthu izi zidachitika m'chipindamu:

- a) Mgezenge adamuyamikira Zikani ndipo adamuza kuti amuyang'ane; asachite manyazi popeza ndi mamuna wake.

- b) Zikani adamuyankha kuti iye ndi bambo wopanda manyazi komanso iye ndi mlamu wake.
- c) Mgezenge adamuza Zikani kuti panthawiyi sanalinso mlamu wake koma mamuna wake popeza adasinthidwa. (Chimanga akachigaya sichikhalabe chimanga.) Zikani adatsindika kuti sankafuna konse.
- d) Mgezenge adati anthu aakazi amanena zinthu zaukwati ngati sakufuna. Atamufunsira Nagama sadalole komabe adamukwatira. Zikani adakanitsitsa kuti sankamufuna Mgezenge.

Pambuyo pake, Nagama adalowanso m'chipindamo nauza Mgezenge ndi Zikani kuti iye akagona m'chipinda china; Zikani akalowe m'chipinda chachikulu akayale.

- e) Zikani adatsindika kuti Mgezenge sangakhale mamuna wake pazifukwa izi:
 - i. Sanayezetse magazi kuti aone ngati ali bwino kapena ayi. Mchemwali adakhala akudwala kwa nthawi yayitali koma sanali kudziwa chomwe ankadwala.
 - ii. Zimaonetsa kuti Mgezenge ndi Nagama amaopa kuyezetsa magazi.
- f) Zikani adauza Mgezenge kuti iye adayezetsa ndipo adamupeza ndi kachirokoyambitsa Edzi. Apa Mgezenge adamuthamangitsa Zikani m'chipindamo.

Zipangizo

Mawu okuluwika

Chimanga akachigaya sichimakhalabe chimanga.



Zikani atachita chikwati ndi Mgezenge adasinthidwa mwakuti sanalinso mlamu wake koma mkazi wake.

Maphunziro m'nunsuyi

1. Kudziteteza

Zikani adatsindika kuti Mgezenge sangakhale mamuna wake pazifukwa izi:

- a) Sanayezetse magazi kuti aone ngati ali bwino kapena ayi. Mchemwali adakhala akudwala kwa nthawi yayitali koma sanali kudziwa chomwe ankadwala.
- b) Zimaonetsa kuti Mgezenge ndi Nagama amaopa kuyezetsa magazi.
- c) Iye adayezetsa ndipo adamupeza ndi kachiroombo koyambitsa Edzi. (Ili lidali bodza.)

2. Kusamala

- Nagama adakhala akudwala kwa nthawi yayitali koma sadaganize zopita kukayezetsa magazi.

NUNSU YACHISANU NDI CHIWIRI

Zikani athawa kunyumba kwa Mgezenge

- a) Mgezenge podzuka m'mawa, sadamuone ndipo atamufunsa Nagama analinso odabwa popeza adawasiya awiriwa m'chipinda chachikulu.
- b) Mgezenge amanena kuti Zikani anakagona kuchipinda limodzi ndi Nagama pamene Nagama adawasiya awiriwa m'chipinda. Pachifukwachi, Nagama adaganiza Mgezenge adapita kukamwa mowa usikuwo.
- c) Adamusakasaka m'zipinda zonse koma sadapezeke.

- d) Anthuwo adazunguzika popeza Zikani adatuluka pamene zitseko zinali zokhoma.
- e) Nagama ndi Mgezenge adaganiza zokamuyang'ana kwa makolo ake.
- f) Mgezenge adauza Nagama kuti sangayende asanadye. Pamawu amenewa Nagama adali ndi maganizo awa:
 - i. Mgezenge akudziwapo kanthu pakusowa kwa Zikani.
 - ii. Nkutheka kuti Mgezenge adamupha mtsikanayu ndipo ngati ndi choncho nayenso anali wokonzeka kuphedwa.

Maphunziro

1. Kukwiya

- Nagama adakwiya pamene Mgezenge adati ayambe wadya asanapite kukamuyang'ana Zikani kwa makolo ake mwakuti adamukalipira Mgezenge kuti ndi mfiti. Kukwiwaku kudachititsa kuti Mgezenge asinthe maganizo.

2. Kusaganiza

- Mgezenge adauza mkazi wake Nagama kuti sangapite kukasaka Zikani asanadye. Izi Nagama adazitanthauzira kuti mamuna wakeyo amadziwapo kanthu pakuti pamene adakana zophikazo Mgezenge adalusa namuopseza kuti akadatha kumumenya.

NUNSU YACHISANU NDI CHITATU

Mkangano pakati pa makolo a Zikani ndi Mgezenge pa kusowa kwa Zikani



- a) Mgezenge ndi Nagama adapita kunyumba kwa makolo a Zikani kuti akamufufuze kumeneko komabe kunalibe.
- b) Makolo a Zikani anali odwabwa pakumva za kusowa kwa mwana wawo ndipo adatulutsa maganizo awa:
 - i. Mgezenge sanayenere kukawafunsa za komwe kunali Zikani popeza anali mkazi wake, adampatsa ndipo ankakhala naye.
 - ii. Ngati adamupha Zikani nkutengako zizimba akadanganena.
 - iii. Munthu akakwatira mkazi amakhala kwa mamuna wake osati kwa makolo ake.
 - iv. Mgezenge sanayenere kumufunsa Nagama za Zikani pamene Zikaniyo adagona m'chipinda chimodzi ndi iyeyo (Mgezengeyo).
- c) Mgezenge adauza makolo a Zikani kuti sakadakamba zoti Zikani adaphedwa pamene mtembo wake sadawuone.
- d) Mgezenge ndi apongozi ake onse awiri adagwirizana kuti akanene kupolisi za kusowa kwa Zikani.

Zipangizo

1) Zifanifani

- a) Ndikamadya masamba osathira nsinjiro ndimakhala ngati mbuzi yomwe ikudya msipu.
- b) Osamangoti maso tunguluzutunguluzu ngati birimankhwe.
- c) Iwensu usangokhala ndwii ngati akukuvinira chinamwali.

2) Mikuluwiko

- a) Pamudzi pakhala zitsiru mkamwini asamakulirepo mwendo.
 - Mgezenge anayenera kupereka ulemu kwa apongozi pamene anawapeza pakhomo pawo posatengera kuti anali amphawi.
- b) Nkhuyu zodya mwana zidapota akulu.
 - Chilichonse chomwe chidachitika pa Zikani chidakhudzanso makolo ake. Pamene Zikani adasowa, makolo ake adasowa mtendere ndipo adagwirizana ndi Mgezenge kuti akanene ku polisi.

3) Mvekero

- a) Tunguluzutunguluzu : kuyang'ana uku ndi uku
- b) Ndwii: kukhala osayankhula koma kumangoyang'anitsitsa

4) Msemphano

Mwana akalirira fupa, muninkhe. Likamuthyola dzino, ndi zake zimenezo.

- Zikani sadawumirire kukwatiwa ndi Mgezenge; adamuwumiriza ndi makolo ake mwakuti pamene adasowa Mgezenge ndi makolo ake anayenera kumusakasaka.

Maphunziro m'nunsuyi

1) Kupanda ulemu

- Mgezenge adafika ndi ukali pakhomo pa apongozi ake komanso ankayankhula ali chilili.

2) Kusokonezeka



- Nangama ankakanika kuyankha mafunso atapita kwa makolo ake popeza adasokonekera ndi kusowa kwa mchemwali wake Zikani.

NUNSU YACHISANU NDI CHINAYI

Anthu akhudza maliro a Zikani ngakhale iye sadamwalire

Ngakhale anthu sadaone mtembo wa Zikani, adakhulupirira kuti adamwalira.

Umboni woti Zikani adamwalira

Panalibe umboni weniweni woti Zikani adamwalira. Anthu adakhulupirira izi:

- Atsikana awiri omwe ankakhala m'nyumba yomwe alonda ankhalango adayisiya ndipo zinkamveka kuti adathawa mabanja awo ndipo m'modzi mwa iwo ankati ndi Zikani, adaphedwa ndi afisi ndipo kunali kovuta kuzindikira nkhope zawo. Matupi awo adalibe ziwalo zina.

Umboni woti atsikana omwe ankakhala m'nyumba yam'nkhalango adamwalira

- Patapita masiku angapo afisi adavuta m'midzi yoyandikana ndi nkhalangoyo.
- Sabata idatha atsikanawo asadaonekenso.
- Anthu adamva fungo loyipa kuchokera kunkhalango ndipo atalowa m'nkhalangomo adapeza matupi awiri ataonongeka kwambiri. Matupiwo adali a atsikana.

Umboni woti m'modzi wa atsikanawo anali Zikani

- Mphekesera zinamveka kuti atsikanawa ankapita ku sukulu zosiyanasiyana nkumakauza atsikana anzawo za ufulu wa maphunziro a atsikana. Izi ndi zomwe Zikani adauzanso makolo ake pamene ankamuuza zoti akwatiwe ndi mlamu wake Mgezenge.
- M'modzi mwa iwo ankafanana ndi Zikani.
- Atsikanawo atafunsidwa mayina awo, adakana kutchula powopa kuti angakawabwezere kumabanja komwe adathawa. Panthawiyi nkuti Zikani atathawa kubanja kwa Mgezenge.

Kumbutso:

- Malingana ndi wotsogolera mwambo wamaliro a Zikani zidali zokayikitsa ngati m'modzi mwa atsikana omwe adaphedwa ndi afisiwo anali Zikani popeza nkhope zawo zidadyedwa kotero kuti kunali kovuta kuwazindikira kuti adali yani ngakhale panali madiresi omwe anthu ankati anali a atsikanawo.
- Anthu adakhulupirira kuti afisiwo adali a munthu ndipo kuti mwiniyo anali Mgezenge.
- Mwa mwambo wake, popeza mtembo wa Zikani panalibe, amuna angapo adapita kumanda n'kukakwirira thunthu lanthochi m'denje lamanda poopa kuti mzimu wa malemu Zikani ungawasautse m'mudzimo.
- Amfumu adachitira umboni kuti Zikani anali mwana wamakhalidwe abwino.

Zikani atulukira pamaliro ake

- Adatulukira pamodzi ndi mzake.
- Mgezenge, Abiti ndi a Gama adamuona.



- c) Mgezenge adachita mantha poyesa ndi muzukwa.
- d) A Gama, bambo ake, adalimba mtima n'kumuyandikira komanso kumugwira kenako n'kuthawa.
- e) Amfumu adamuponyera dothi kuti awone ngati ndi muzukwa kapena munthu weniweni popeza muzukwa umazimirira akawuponyera dothi. Zikani sadazimirire.
- f) Atate ake, a Gama, adafuna kudziwa kuti zidatheka bwanji munthu wakufa n'kudzukanso.
- g) Iye adatsindika kuti iye simalemu ndipo pamoyo wake sadafepo; ndi mwana wa Mulungu yekha basi yemwe adadzukapo.
- h) Mgezenge adakuwa kuti mkazi wake sadafe; adali ndi moyo koma Zikani adakanitsitsa kuti sadali mkazi wake. Iye adasowa chifukwa ankamuthawa Mgezengeyo.
- i) Adanena mosaopa kuti Mgezenge ndi chidyamakanda, munthu woyipa komanso wopusa. (Adali ngati nkuku yodzimwera mazira ake omwe popeza adamulera yekha Zikani kenako n'kumafunanso akhale mkazi wake.)

Mawu a Zikani pa nkhani ya atsikana omwe adaphedwa ndi afisi

- a) Matupi omwe adapezekawo anali a atsikana anzake omwe adathawa kumabanja okakamizidwa. Nawonso adathawa mwambo wa shazi ndi amuna adyera monga Mgezenge.
- b) Zovala zake zidapezeka ndi atsikanawo popeza sadapeze mpata wotenga zovala zawo pamene ankathawa kumabanjako mwakuti Zikaniyo ndiye adawabwereka zake.

- c) Atsikanawa, Sibongile ndi Malita, adaphedwa ndi afisi atangochapa zovala zawo. Iye ndi mnzake, Chisomo, adapulumuka popeza adathawira kutali atangomva phokoso la afisiwo. Iwo adathawira kwa mayi wina wopemphera yemwe adawalimbikitsa kupempherera mizimu ya anzawo awiriwo.
- d) Atamva kuti anthu akulira maliro ake, iye adabwera mwansanga kuti anthu adziwe zoti iye adakali moyo.

Tsoka la mnzake wa Zikani (Chisomo Mwayikale)

- a) Makolo ake anakongola ndalama kwa mutnhi wina wolembera dzina lake Mwenekuchanya.
- b) Atalephera kubweza ndalamazo, makolowo adagwirizana ndi Mwenekuchanya kuti Chisomo akhale mkazi wake wachinayi ngakhale anali wachichepere kwambiri (ali ndi zaka zisanu).
- c) Makolowo adakamupereka kwa njondayi (Mwenekuchanya) ali sitandade 7. Mwambowu umenewu umatchedwa “Kupimbila” kapena “Kupawila”.
- d) Iye adathawa tsiku lomwelo ndipo adakwera basi ngakhale adalibe ndalama. Atawafotokozera anthu zomwe zidamchitikira, adamuthandiza. Iye ankati akupita kwa amalume ake kuboma ngakhale kuti komwe ankawera sankakudziwa. Mwamwayi adakumana ndi Zikani atangotsika basi ndipo adayamba kukhalira limodzi.

Mawu a amfumu atamva nkhani ya Chisomo

- a) Atamva izi adati adachita manyazi nati sadayenerere kuloleza ukwati wa Zikani kuti uchitike.

- b) Adauza anthu onse kuti miyambo yina n'kutheka idali yabwino pachiyambi koma anthu adayisokoneza. N'kuthekanso makolo ena anali adyera. Miyambo ina mwina idayamba makolo atasauka.
- c) Adalamula kuti miyambo monga hlazi (shazi)/mbirigha/isakulwa/chimeta masisi ithere tu m'mudzimo.

Mgezenge ayambitsa chisokonezo.

- a) Iye adatsindika zomutengabe Zikani kukhala mkazi wake ngakhale zikadavuta motani.
- b) Adati anthu ena adadya ndalama zake choncho adayenera kubweza.
- c) Mgezenge adati miyamboyoyi ikamatha, iye akhala atamutenga mkazi wake, Zikani. Kupanda kutero akadavulaza munthu wina. Iye adaopseza kuti kusintha miyambo kusayambire pa iyeyo.

Maphunziro m'nunsuyi

1) Ana adazunzika kamba ka umphawi wamakolo

- a) Makolo a Chisomo adamukwatitsa ali wachipere kwa mkulu yemwe adakanika kumubwezera ndalama zake atakongola. Izi zidachititsa Chisomo kuti athawe n'kumakakhala m'nyumba ina yomwe adayisiya alonda ankhalango. M'nyumba m'menemu ndi momwe anzawo ena awiri adaphedwa ndi fisi.
- b) Zikani adathawa ku banja lokakamizidwa ndipo ankakhala m'nyumba ina yomwe adayisiya alonda ankhalango. Afisi atavuta m'midzi yoyandikana ndi nyumba, adapha anzawo awiri.

2) Chisoni

- Anthu omwe adamva nkhani ya Zikani adamuthandiza kuti ulendo wake upitirire.

3) Chikondi

- Zikani adawabwereka zovala atsikana omwe adaphedwa ndi afisi popeza pobwera kwawo sadatenge zovala.

4) Nkhanza

- Makolo a Zikani ndi Chisomo adakwatiwitsa ana awo mowakakamiza asadafike pamsinkhu woyenera kutero.

5) Kudziteteza

- Zikani ndi Chisomo adathawa ku mabanja okakamizidwa komanso adathawa afisi olusa napita kwa mayi wina komwe ankapempherera mizimu ya anzawo awiri amene adaphedwa ndi afisiwo.

6) Kulongosola/Kuwongola zinthu

- Amfumu adathetsa mwambo wa shazi/ mbirigha/ isakulwa/ chimeta masisi

7) Kuipa mtima/Kusamva

- Mgezenge adalimbikira zoti amutengabe Zikani ngati mkazi chonsecho amfumu adalengeza kuti adathetsa mchitidwe wa shazi m'mudzi mwawomo.

Zipangizo

Zining'a



Wokhupuka: Wolemera.

Matanthauzo amawu

Kupimbila/Kupawila

- Mchitidwe wokwatiwitsa mwana wachichepere pamene makolo alephera kubweza ngongole yandalama.

NUNSU YAKHUMI

Sukulu ipindulira Zikani, Funsani ndi Chisomo

- Anthu atatuwa adaphunzira ndipo adali pantchito. Chisomo ankagwira ntchito limodzi ndi Zikani m'bungwa la “Mtetezi wa Mwana” lomwe adayambitsa Zikani.

Macheza a Chisomo ndi Funsani

- Chisomo adafika kunyumba kwa Funsani ndi Zikani kuti akapereke lipoti lantchito yomwe adakagwira ku esiteti ina komwe zimamveka kuti mwini wake ankagwiritsa ntchito ana aang'ono.
- Chisomo adasankha kupatsidwa madzi m'malo mwa chakumwa chilichonse ndipo adati:
 - ✓ Zakumwa zisamakhale ndi shuga wambiri komanso zothiramo zosadziwika.
 - ✓ Agogo ake adawadula mwendo ndipo matenda ashuga ndiwo adali gwero.
- Funsani adauza Chisomo kuti kusankha madzi isakhale njira yopulumutsira makobili pozemba zakudya zabwino popeza atsikana makobili amathera m'mutu.

Macheza a Chisomo, Zikani ndi Funsani

- Chisomo adauza Zikani kuti adabwera kudzamuza m'mene adayendera ku esiteti komwe kudamveka kuti mwini wake akugwiritsa ntchito ana aang'ono.
- Adakumbutsana zakale ndipo adakamba zotsatirazi:
 - ✓ Akadapanda kuchita khama bwenzi panthawiyi atakalamba; sakadaphunzira monga adachitira panthawiyi.
 - ✓ Sukulu ndi yabwino popeza idathandiza kuti ayambitse bungwe la “Mtetezi wa Mwana”.
- Matenanti a ku esiteti ina adakadandaula ku ofesi ya Zikani ndi Chisomo. M'modzi mwa matenantiwo adali ndi ana asanu ndi awiri. Onsewo amagwira ntchito pa esiteti pomwepo. Anawo ankavutika popeza ankagwira ntchito zolemetsa komanso sankapita kusukulu.
- Funsani adakumbukira m'mene ankagwirira ntchito kugolosale kwa a Mgezenge: amagwira ntchito n'kumalipidwa zovala zakale.
- Zikani adagwirizana ndi Funsani kuti Zikani adachita bwino kuthawa kwa a Mgezenge popeza a Mgezenge adali kudwaladwala mwakuti adaonda kwambiri ndipo mkulu wake adamwalira. Chuma chonse chidatha: ng'ombe zidathera malipiro asing'anga, golosale adatseka.
- Zikani adalakalaka akadathandiza makolo ake koma panthawiyi anali atamwalira.

Zotumphuka pa macheza a Zikani, Funsani ndi Chisomo kunyumba kwa Funsani ndi Zikani

- Chilonda chimavuta kupola ndi matenda a shuga.



- Nsima yamgayiwa ndi yabwino popeza imakhala ndi madeya ofunika m'thupi komanso ili ndi sitalichi ndi faiba wambiri. Nsimayi imathandiza kupewa matenda amtima ndi khansa.
- Patapita nthawi Zikani adakwatiwa ndi Funsani
- Zikani adayambitsa bungwe la 'Mtetezi wa Mwana' ndipo anali bwana wamkulu. Chisomo adali mthandizi wake.
- Azungu a mishoni ndi omwe adalipirira sukulu Funsani mpaka ku yunivesite ndipo adamupezeranso ntchito. Azunguwa adapita kumwambo wolandira madigiri monga makolo a Funsani. M'modzi mwa azungu amishoniwa anali Bambo Alfred.
- Eni esiteti akalemba bambo ntchito, ndiye kuti banja lonse limagwira ntchito yomweyo.
- Eni esiteti anali oyipa pazifukwa izi:
 - ✓ Ndi iwo okha amene amagula fodya wamatenanti.
 - ✓ Amagula fodya wamatenanti pa mtengo wozizira.
 - ✓ Amalamula mtengo wogulira fodya wamatenanti awo.
 - ✓ Amawapatsa matenanti zakudya zosakwanira.
- Makolo a Zikani komanso Funsani anali atamwalira panthawiyi.
- Zikani ndi mamuna wake Funsani ankacheza moserewulana.
 - ✓ Zikani adanena moserewula za ntchito yakale ya Funsani: "Ikakhala golosale yako ija muli akangaude okhaokha."

- ✓ Funsani adanena moserewula za ukwati wa Zikani ndi Mgezenge: "Amuna ako aja anali wovuta kwambiri."

Zipangizo

1) Zining'a

- a. Fisi asanathyole khola
 - asanagonane
- b. Anatsikira kulichete.
 - Anamwalira
- c. Ali mafupa okhaokha
 - Adaonda kwambiri.
- d. Ndi bwenzi wa mphasa.
 - Akudwaladwala.
- e. Onse anatsogola.
 - Anamwalira.
- f. Pamtego wozizira
 - Pamtego wotsika
- g. Makobiri akuthera m'mutu.
 - Makobiri akuthera kukonza tsitsi.
- h. Tawonjola ana ambiri.
 - Tapulumutsa ana ambiri.

2) Chifanifani

- Ndinkakhalira mphanthi ngati nsikidzi.
- ✓ Ndinkakhala movutika kwambiri.

Maphunziro m'nunsuyi

1) Chikondi

- Azungu amishoni adamutenga funsani makolo ake atamwalira n'kumakhala naye ndipo adamulipirira sukulu mpaka ku yunivesite. Atatsiriza ku yunivesite, adamupezera ntchito.

2) Nkhanza

- A Mgezenge ankamugwiritsa ntchito Funsani ku golosale koma ankamulipira zovala zokutha.
- Eni esiteti
 - ✓ ndi iwo okha amene amagula fodya wamatenanti.
 - ✓ amagula fodya wamatenanti pa mtengo wozizira.
 - ✓ amalamula mtengo wogulira fodya wamatenanti awo.
 - ✓ amawapatsa matenanti zakudya zosakwanira.
 - ✓ amagwiritsa ntchito ana aang'ono.
 - ✓ akalemba ntchito bambo, banja lonse limagwira ntchito yomweyo.

3) Kukonda/Kusamala ntchito

- Zikani adafuna kumva kaye m'mene Chisomo adayendera ku esiteti komwe kudamveka kuti mwini wake akugwiritsa ntchito ana aang'ono. Adachita zimenezi atangofika kuchokera kuntchito, asadapume ngakhale mamuna wake Funsani adamuza kuti ayambe wapuma.

4) Kudziwa zinthu

- Chisomo adachenjeza Funsani pa nkhani ya zakumwa zashuga wambiri komanso zothiramo zosadziwika. Adamufotokozeranso za matenda a shuga ndi momwe

adachititsira kuti agogo ake adulidwe mwendo. Mtsikanayu adafotokozanso za kufunika kwa nsima yamgayiwa.

NUNSU YAKHUMI NDI CHIMODZI

Zikani ndi Chisomo ku esiteti

- Adafika pakhomo pa a Kamwendo atavala zitenje ndi mipango ndipo adalonjeredwa. Bambo Kamwendo anali tenanti.
- Ataona mwana wina wa a Kamwendo atasenza mtolo wankhuni waukulu kuposa msinkhu wake, Zikani adafunsa modabwa popeza mnyamatayo anayenera kukhala ali kusukulu panthawi monga imeneyi.
- Zikani adawafunsa chiwerengero cha ana omwe adali nawo komanso momwe amaliwonera tsogolo lawo ndipo a Kamwendo adayankha izi:
 - ✓ Ali ndi ana asanu ndi awiri.
 - ✓ Mwana amene adadutsa ndi mtolo anali wachinayi.
 - ✓ Ana ena anali kuganyu yopalira.
 - ✓ Mwana wawo wamkazi adapita kutauni kukagulitsa masamba.
 - ✓ Ana awiri aang'ono adaperekeza mayi awo kuchigayo.
 - ✓ Anawo sakadamapita kusukulu tsiku lililonse popeza sakadapezako chakudya.
 - ✓ Amawaphunzitsa anawo momwe angadzakhalire akadzakula; amawaphunzitsa ntchito.

Zomwe Zikani adaunikira a Kamwendo koma sadazimvetse

- Ntchito zomwe ana aang'ono amagwira pakhomu zizifanana ndi msinkhu wawo.
- Kholo logwiritsa ana ntchito zoipa litha kumangidwa.
- Dziko lidasainira mgwirizano pa 17 June 1999 wa 'Mitundu ya Ntchito Zoyipitsitsa kwa ana' "Worst Forms of Child Labour Convention" womwe gawo 3d limakamba za ntchito zomwe zingatse kuononga moyo wamwana pa thanzi, makulidwe, makhalidwe ndi maganizidwe aumunthu.
- Zimaonetsa kuti a Kamwendo sakulera bwino ana: samawapititsa kusukulu nthawi zonse, amawagwiritsa ntchito zomwe zikadatha kuononga moyo wawo. Chitsanzo chinali cha mwana amene adadutsa ndi mtolo wankhuni yemwe amaoneka kuti adakakamizidwa kutero.

A Kamwendo adawathamangitsa Zikani ndi Chisomo ponena kuti sangawalamulire za ana awo poti iwo adalibe ana komanso sankadziwa chilichonse chokhudza mwana.

Maphunziro m'nunsuyi

1. Kusazindikira

- A Kamwendo ankagwiritsa ntchito ana awo mobzola msinkhu wawo komanso ankawajombetsa kusukulu nthawi zambiri. Mayankho awo pamafunso omwe Zikani adawafunsa, monga "ana sapita kusukulu tsiku lililonse popeza sangakapezeka zakudya", adasonyeza

kuti sankazindikira kufunika kwa sukulu komanso kuti ankawachitira nkhanza anawo.

2. Kusaphunzitsika

- A Kamwendo sadamvetse kuti kugwiritsa ana awo ntchito mopitirira mulingo ndi kuwachitira nkhanza. M'malo mwake iwo adatanthauzira kuti Zikani ankawauza kuti anawo asamagwire ntchito mwakuti adamulalatira namuopseza kuti achoke pakhomu asadamukhwiyitsire agalu.

3. Kuteteza

- Zikani adayambitsa bungwe la "Mtetezi wa Mwana" kuti awonjole/apulumutse ana kumavuto a kugwiritsidwa ntchito zosagwirizana ndi msinkhu wawo komanso kusapita kusukulu.

NUNSU YAKHUMI NDI CHIWIRI

Mgezenge kunyumba kwa Zikani ndi Funsani

- Adafika akudziyankhulira zinthu izi:
 - ✓ Abale ake onse adamwalira.
 - ✓ Adali wolemara koma zinthu zonse (mbuzi, ng'ombe, sitolo, nkuku ndi nkunda) zidatha.
 - ✓ Pa esiteti yake boma lidamanga sukulu ndipo ndalama zachipukutamisozi sidatha kalekale.
 - ✓ Msewu womwe udadutsa m'munda mwa apongozi ake umalunjika kusukulu.
 - ✓ Anthu akamuona, ankamutcha wamisala kapenanso sing'anga.

- Adaganiza zopempha malo ogona panyumba ina yomwe sankadziwa kuti inali ya Funsani ndi Zikani.
- Adachita odi ndipo Chisomo Mwayikale ndiye adamulonjera.
- Adamuza Chisomo kuti akawauze eni nyumba kuti iye ankafuna malo ogona; tsiku lotsatiralo azipita.
- Chisomo adauza Mgezenge kuti mnzakeyo adavomera kuti amusunga ndipo akagona kunyumba yogona anyamata. Adamutengera Mgezenge kunyumba yayikulu kuti akamuone.
- Funsani adawazindikira a Mgezenge ndipo Chisomo adawadziwanso koma iwo sadawazindikire.
- Zikani adawadziwitsa a Mgezenge kuti iyeyo ndi Zikani ndipo mamuna wake ndi Funsani.
- Mgezenge adapepesa.
- Funsani ndi Zikani adakhululukira Mgezenge pa zonse zomwe adawachitira.
- Zikani adauza wantchito wake kuti awasamalire a Mgezenge ku chipinda cha alendo.
- Chisomo adatsanzika n'kumapita kwawo.

Zipangizo

Zining'a

- a) Onse kutha psiti
 - Onse kumwalira
- b) Ndiwone msana wanjira
 - Ndizipita

Maphunziro m'nunsuyi

1. Kunong'oneza bondo

- Mgezenge adadziyankhulira yekhayekha modandaula kuti kunja kuyanja lichero. Iye adali ndi chuma koma chidatha chonse. Abale ake onse adamwalira ndipo anthu akamuona akumunena kuti ndi wamisala komanso sing'anga.

2. Chuma ndi mchira wakhoswe sukhalira kupululuka

- Mgezenge adali ndi chuma chambiri ndipo ankachitira anthu nkhanza. Adagwiritsa ntchito chuma chake kuti akwatire mlamu wake Zikani. Chuma chonsecho chidatha ndipo adasauka mwakuti anthu akamuona ankamuyesa wamisala.

3. Kukhululuka

- Zikani ndi mamuna wake Funsani adamukhulukira Mgezenge ngakhale adawachitira zoyipa. Mgezenge adagwiritsa chuma pofuna kuumiriza makolo a Zikani kuti achite shazi komanso ankamugwiritsa ntchito Funsani kugolosale kwawo koma amamulipira zovala zakutha. Atafika pakhomo pawo atasaukiratu komanso atadwalika kwambiri n'kupempha malo ogona, anthu awiriwa adamusamala Mgezenge.

4. Kusayiwala

- Funsani adakumbukira zonse zomwe Mgezenge adachitira Zikani ndi iye yemwe. Iye adati Mgezenge adali katswiri pogwiritsa ana ntchito yakalavula gaga, Iye adali kapolo wake, adali chidyamakanda ndipo Zikani adatsala pang'ono kufa kamba ka iye.



NUNSU YAKHUMI NDI CHITATU

Mgezenge adzikhweza pakati pa usiku

Wantchito wa Funsani ndi Zikani adayimbira foni Funsani kuti anamva phokoso losonyeza kuti munthu ankaphupha mobanika ndipo atathamangira m'chipinda momwe adagona Mgezenge, adapeza atadzimangirira ndi chingwe choyanikapo zovala.

Funsani ndi wantchito adathandizana kuswa chitseko ndipo adampeza Mgezenge asadafe. Adayitanitsa makiyi a galimoto kuti amutengere kuchipatala.

Chipangizo

Mkuluwiko

➤ Chifundo chidapha nkhwali.

- ✓ Chisoni chomwe Funsani ndi Zikani adachitira Mgezenge pompatsa malo ogona chikadawabweretsera mavuto pamene Mgezenge adadzimangirira.

Maphunziro m'nunsuyi

➤ Kudziweruza

- ✓ Mgezenge adadzimangirira kuti afe popeza kudali kovuta kuti akhale m'nyumba mwa Funsani ndi Zikani poganzira nkhanza zomwe adawachitira pamene iye adali ndi chuma.

➤ Moyo ndi wozungulira

- ✓ Mgezenge adakapempha chithandizo kunyumba kwa Funsani (adapempha malo ogona) pamene

m'mbuyomo Mgezenge ndi amene adalemba ntchito Funsani yogulitsa m'golosale mwake.

Funso loyankha mwachimangirizo

- Ndi zochitika ziti zomwe zikusonyeza kuti Mgezenge anali wankhanza?

MUTU 5

MUDZI WA MFUMU TANDWE

(Wisdom Nkhoma)

Ochita chisudzo

Mfumu Tandwe

Mfumu ya m'mudzi yomwe inkakhulupirira nduna zake ndipo idazigawira maudindo osiyanasiyana

Bambo Tikita

Nduna yayikulu ya mfumu

Bambo Sefani

Nduna ya mfumu

Mayi Amuli

Nduna ya mfumu omwe inkayang'anira za achinyamata komanso kuonetsetsa kuti pasamakhale kusalana

Bambo Lungu

Nduna ya mfumu yomwe inkayang'anira za nkhanza zochitika kwa amayi ndi ana aakazi

Mayi Chibwe

Nduna ya mfumu yomwe inkayang'anira zachilengedwe



Mayi Mwenda

Nduna ya mfumu

Gogo Tsinde

Mlangizi wamkulu wa mfumu

Chiphaliwali

Mtumiki wa mfumu yemwe amakhazikitsa bata panthawi ya mkumano/msonkhano pabwalo la mfumu

Oyimira magulu osiyanasiyana m'mudzi

Anthu am'mudzi

Malo mwachidule

- a) Kubwalo lamfumu
- b) Kupolisi

Kubwalo la mfumu Tandwe

Chiphaliwali adaletsa phokoso ndipo adauza anthu kuti msonkhano udayenera kuyambika.

Cholinga chamsonkhano

- Kukambirana/Kuunikira mfundo zofunika kwambiri m'mudzimo

Mawu amfumu potsekulira msonkhano

- Adayamikira anthu kuti zomwe adagwirizana pamsonkhano ngati womwewu chaka chapitacho zinali kuchitika ndipo anthu andayambapo kuona zipatso zake.
- M'chaka chatsopanochi, anali ndi mitu ingapo yoti akambirane.
- Idayitana nduna zake kuti zifotokoze mitu yomwe idalipo motere:

1. Mayi chibwe (nduna yoyang'anira zachilengedwe)

Adayankhula zinthu zotsatirazi:

- Mudzi wawo unali wochita bwino (wa mwanaalirenji)
 - ✓ Anthu ochokera kumadera ena monga ku Chombo, ku Linga, kwa Kalimanjira, ku Chithiba ndi ku Benga ndi ena ochokera kumapiri ankadzachita nsuma. Anthuwa ankatsata zakudya monga chimanga, mpunga ndi chinangwa.
 - ✓ Nthaka inali yachonde.
 - ✓ Nyanja yawo ya Mthabithabi inali ndi nsomba zambiri monga nthachi, nkhututu, mbununu, chitemera ndi nkhalala.
 - ✓ Kudambo la Mthabithabi kunkamera therere la kazirira.
 - ✓ Nkhalango yam'mudzimo inali ndi zipatso zam'tchire monga kapwati, masuku, nziru, kankhande, maye, nthudza, bwemba, mapoza ndi kasokolowe. Nthawi yadzinja m'nkhalangomu ankazula bowa wokoma kwambiri monga chifisi, manyame, katerera, mnofuwankhuku ndi nkwayukwayu.
 - ✓ M'mudzimo munali mitengo yamankhwala amakolo monga mvunguti, msolo, kamphoni, msambamfumu, mwavi ndi thundu. Mitengo ina ndi monga m'bawa, mlombwa, mng'wenya, mgwalangwa, msopa, mkongomwa ndi mkalati.
 - ✓ M'nkhalango yam'mudzimo munalinso nyama monga akalulu, agwape ndi ntchenzi.

- Zinthu zonse zidatha pazifukwa izi:
 - ✓ Nkhuli (kukonda kudya zankhuli)
 - ✓ Kuotcha makala
 - ✓ Kucheka matabwa ndi kusema ziboliboli
- Zotsatira zamchitidwewu ndi izi:
 - ✓ Kusintha kwa nyengo:
- Mvula ikugwa mwanjomba
- Ngozi zachilengedwe zidachuluka m'mudzimo
- Mlangizi wamkulu, Gogo Tsinde, adakumbutsa anthu onse kuti mfundo pa zoyenera kuchita zikakambidwa m'malimana ndipo adzakumananso Loweruka pakatha sabata ziwiri ndipo kuti limana lililonse lidzafotokozera bwalo mfundo zake.

Asanadzutse Bambo Lungu, amfumu adayitanitsa gulu lovina la amayi ndi atsikana kuti ayimbe komanso avine nyimbo imodzi yokamba za kuonongeka kwa chilengedwe komanso kusintha kwa nyengo.

2. Bambo Lungu (nduna yoyang'anira za nkhanza zochitikira amayi ndi ana aakazi)

Ndunayi idayankhula motere:

- Nkhani zokhudza nkhanza zomwe ankangomva ngati nkambakamwa chabe zidayamba kuchitika m'mudzimo.
- A Chiphiri adamangidwa atamenya mkazi wawo woyembekezera mpaka mkaziyo adapita padera.

- Amuna ambiri akagulitsa tsabola amalowerera ku Dwangwa. Amakaononga ndalama ndi akazi oyendayenda. Zikatha ndalamazo mpamene amabwerako. Ku Dwangwa amabwerako alibe kalikonse komanso atatenga matenda opatsirana pogonana.
- Akazi amavutika nkugwira ntchito koma amuna amakadya ndalamazo ndi akazi ena.
- Anthu ambiri ofunikira m'mudzimu, anali atamwalira ndi matenda a edzi.
- Bambo Pedegu adamangidwa kamba ka kugwirira mwana wawo wompeza wazaka khumi.
- Pasukulu yomwe adayandikana nayo padali aphunzitsi ena aamuna omwe ankafunsira tiana tatikazi.
- Adapempha malimana kuti akaunikire mozama zedi nkhanzi ya amayi ndi atsikana
- Adatsindika kuti mchitidwe wankhanza utha chaka chimenecho.

Pasanalowe mayi Amuli ndi nkhanzi zina ziwiri, amfumu adayitanitsa gulu lovina la abambo komanso la anyamata la Kanada kuti avine nyimbo imodzi yomwe imakamba za kuipa kwa nkhanza kwa amayi ndi ana.

3. Mayi Amuli (nduna yoyang'anira nkhanzi za achinyamata ndi kuonetsetsa kuti pasamakhale kusalana)

Ndunayi idayankhula nkhanzi zitanu motere:

a) Makhalidwe a anyamata ndi atsikana

- Kale anthu ankati achinyamata ndi atsogoleri amwa.
 - Makono amati achinyamata ndi atsogoleri alero komanso amawa popeza:
 - ✓ Makono ali m'maudindo ndipo akutsogolera pa zochitika zosiyanasiyana.
 - ✓ Adakali anthete ndipo ali ndi zaka zingapo kutsogolo; dziko lidzakhalabe m'manja mwawo. Makolo monga iwowo adatsala pang'ono kumwalira.
 - Akadzamwalira, achinyamata adzasunge mawu awo.
 - Anyamata ambiri m'mudzimo adalowerera komanso adasochera:
 - ✓ Amangokhalira kumwa mowa ndi mankhwala ozunguza bongo. Ambiri mitu yawo sinkayenda bwino.
 - ✓ Anyamata angapo m'mudzimo adachita misala kamba ka kukhwewa/kusuta chamba.
 - Atsikana sankavala bwino m'mudzimu:
 - ✓ Ankavala kazimoto/ndekesha (zovala zazifupi kwambiri) pamaliro nkumakanika kukhala pansi.
 - ✓ Atsikana amayenda bere lili pamtunda ngati logulitsa.
 - Achinyamata analibe chidwi ndi makhalidwe abwino amakolo
 - Miyambo yakale yoipa idathetsedwa.
- b) Achinyamata ndi ndale**
- Achinyamata amatengeka ndi zandale, makamaka nthawi yamisonkhano yokopa anthu.

- Akasuta chamba komanso akamwa kachasu, amayambitsa chipolowe.
- Zipolowe zomwe adachita tsiku lina zidaphetsa anzawo ophunzira bwino ndipo makolo awo anali kusowa mtengo wogwira kamba ka imfa yawo.
- Ana a atsogoleri azipani sachita nawo zipolowe ndipo amakhla otanganidwa ndi maphunziro kuti nawonso adzawalamulire.

c) Kusalana

- Anthu ena anali kusolidwa pazochitika za m'mudzimo kamba ka kuti ndi amtundu wina kapena chimbedzo china.
- Anthu ankasolidwa pantchito monga kulima msewu, zomwe amalandirapo ndalama komanso pa zinthu zaulere monga kulandira chakudya chomwe mabungwe apereka kwa anthu ovutika.
- Mayiwa adafotokoza ndi chitsanzo kuti mwana akabadwa kuchipatala onena uthenga samati kwabadwa Mkhirisitu, Msilamu, Mkunja Kapena Mchewa, Myawo ndi Mlomwe kapena Mtumbuka. Chimodzi wopereka uthenga wamaliro sasiyanitsa.
- Sukulu yamm'udzimo inali yampingo koma ophunzira ake anali amipingo yosiyanasiyana osati mpingo wa eni sukuluwo. Aphunzitsinso anali amipingo yosiyanasiyana. Chimodzimodzi, chipatala cham'mudzimo chinali champingo koma ogwira ntchito ndi olandira thandizo anali amipingo yosiyanasiyana.

- Anthu amipingo ndi mitundu yosiyana amadalirana; n'chifukwa chake akuyenera kukhalira limodzi komanso kugwira ntchito limodzi.
- Anthu amene amalimbikitsa za sankho ndi opanda nzeru komanso osaganiza mozama.

Amfumu adauza gulu lonse kuti mfundo zomwe zinalipo zinali zokhazo ndipo adapempha Gogo Tsinde kuti awakumbutse anthu mfundo zomwe zidakambidwa pamsonkhanowo. Gogo Tsinde adawuza Mayi Mwenda omwe adafotokoza mwachidule mfundo zamsonkhano.

Pambuyo pa zonse panali chidyerano. Aliyense amadya chakudya chomwe adatenga pamodzi ndi anthu ena osati abale ndi anansi ake.

Gogo Tsinde adakumbutsa anthu kuti akatsiriza kudya apite m'malumana mwawo kuti agwirizane tsiku loti akumane ndipo akambirane zomwe adamva pamsonkhanowo. Pavuto lililonse apeze magwero osachepera atatu komanso akambirane momwe angalithetsere vutolo. Nduna zamfumu zidzayendera malimana kuti zione m'mene zinthu zikuyendera.

Mfumu Tandwe idatseka zonse pokumbutsa anthu kuti adzakumananso Loweruka pakapita sabata ziwiri ndipo lumana lomwe silidzapezeka lidzapereka mbuzi imodzi.

Zipangizo

1. Zining'a

a. Kuchita kaliunji

- Kukumana
- b. Tigundane mitu
 - Kukambirana mokuya
- c. Waziwala m'maso
 - Wamisala
- d. Amvula zakale
 - Akale
- e. Anagonera dzanja
 - adamwalira
- f. Anadula phazi
 - Anasiya kubwera pamalo
- g. Zooneka ndi maso
 - Zodziwika bwino
- h. Ikugwa mwanjomba
 - Ikugwa yochepa komanso mwa apo ndi apo
- i. Taima mitu
 - Tadabwa kwambiri
- j. Anapita padera
 - Adabereka mwana wakufa.
- k. Kukhalira m'mphanthi
 - Kukhala movutika komanso mwamantha kwambiri
- l. Mwabwerako manja ali m'khosi
 - Mwabwerako opanda chilichonse
- m. Adatsikira kumsitu
 - Adamwalira
- n. Dzuwa latsala pang'ono kutilowera
 - Tatsala pang'ono kumwalira.
- o. Kumbiya zodooka
 - Kumanda

- p. Kukhwewa
 - Kusuta
- q. Zikutidulitsa mutu wazizwa
 - Zikutidabwitsa
- r. Kuzitengera pamgong'o
 - Kuchita zinthu mosazimvetsa bwino komanso mopitiriza muyeso
- s. Zoyika moyo pachiswe
 - Zoti zikhoza kuononga moyo
- t. Ukadziwotche
 - Kulimba mtima kololera ngakhale kufa
- u. Mutayabwidwa ndi chitedze
 - Mutatenga matenda opatsirana pogonana.

2. Mikuluwiko

- a. Chala chimodzi sichiswa nsabwe. /Mutu umodzi susenza denga.
 - Munthu sangachite zinthu yekha; amathandizana ndi ena.
- b. Mawu a akulu akoma akagonera.
 - Mawu a akulu amadzapherezero pakapita nthawi.

3. Mvekero

- a. Mbalambanda: kuonekera
- b. Mbwandawumbwandawu: kuyenda motopa

Maphunziro

1. Nkhanza

- a. A Chiphiri adalekerera mkazi wawo woyembekezera ndipo ali wolema kuti akatole nkhuhi kudondo.

- b. A Chiphiri adamenya mkazi wawoyu pamene adabwera mochedwa kuchokera kunkhuniku.
- c. Bambo Pedegu adagwirira mwana womupeza wazaka khumi.
- d. Azibambo akagulitsa tsabola, amapita ku Dwangwa kukusakaza ndalama ndi akazi oyendayenda chonsecho ankalima ndi akazi awo. Akabwerako ku Dwangwako alibe kalikonse komanso atatenga matenda opatsirana pogonana amafuna akazi awo kuti awadwazike.
- e. Mamuna wina adafuna kugwirira mayi ake omubereka.

2. Mudzi wa mfumu Tandwe unali wadongosolo

- Mfumu Tandwe simagwira ntchito yokha. Idagawira nduna zake zochita ndipo nduna iliyonse imagwira ntchito yake molumikizana ndi akuluakulu a m'malimana. Pamsonkhano, aliyense amatsatira ndondomeko yamalonje poyankhula.

3. Chikondi

- a. Mayi Pedegu adapita kukawazonda amuna awo kundende ngakhale adamangidwa kamba kogwirira mwana wawo womupeza.
- b. Atsogoleri m'mudzi mwa Mfumu Tandwe adathetsa miyambo yakale yamokolo yoyipa monga kulowa kufa, chokolo komanso kupondereza azimayi.

4. Kusunga chinsinsi



- Azimayi ena amabisa amuna awo akagwirira ana aakazi.

5. Mchitidwe wosasiyanitsa amuna ndi akazi (gender)

- Mfumu Tandwe idali ndi nduna zazimuna komanso zazikazi ndipo mlangizi wamkulu ndi ena oyendetsa zinthu panthawi yamsonkhano adali akazi.

6. Kuganiza molakwika

- Makolo a anyamata omwe adapenga ndi chamba ankaganiza ndipo ankayankhula kuti anyamatawo adalodzedwa ndi nkhalamba.

7. Kusalana

- Anthu a m'mudzi mwa Tandwe, omwe anali osiyana zipembedzo ndi mitundu yomwe ankapita ku sukulu ndi chipatala cha mpingo ngakhale kuti zinthu ziwirizi zinali za mpingo wosiyana ndi anthuwo.

8. Kulowerera

- Achinyamata a m'mudzi mwa mfumu Tandwe anali osokonekera. Ankasuta chamba, ankamwa kachasu ndipo ena adapenga. Ankatengeka ndi zandale makamaka pamisonkhano yokopa anthu mwakuti ankayambitsa chipolowe ndipo pachipolowe china anzawo enaophunzira bwino adaphedwa. Atsikana ankavala zazifupi kwambiri ngakhale pamaliro mwakuti ankakanika kukhala panso komanso ankavala zoonetsa mabere.

9. Kusasamala

- Anthu a m'mudzi mwa Tandwe adadula mitengo pocheka matabwa, kuotcha makala komanso kusema ziboliboli mwakuti ana amakono mitengo yachilengedwe yamankhwala amakolo monga mvunguti, msolo, kamphoni, msambamfumu, mwavi ndi thundu komanso ina monga m'bawa, mlombwa, mng'wenya, mgwalangwa, msopa, mkongomwa ndi mkalati sankayidziwa. Mchitidwe wodula mitengowu udadzetsa mavuto a kusintha kwa nyengo kugwa kwa mvula mwanjomba komanso kuchuluka kwa ngozi zachilengedwe m'mudzimo.
- Anthu ankawedza nsomba mwadyera choncho zambiri zidatha. Nyanja yawo ya Mthabithabi inali ndi nsomba zambiri monga nthachi, nkhututu, mbununu, chitemera ndi nkhalala.

10. Kuganiza mwakuya

- Amfumu amayitanitsa gulu la ovina monga amayi ndi atsikana komanso abambo ndi anyamata a Kanada pambuyo pa zoyankhula za nduna. Izi zimathandizira kuti anthu asatope komanso asanyinyirike kusalika kwa msonkhano. Izinsu zimapereka mpata kwa woyankhula kuti akonzekere.

Mafunso oyankha mwachimangirizo

1. Malingana ndi zochitika m'bukhu la *Chamdothe* ndi zisudzo zina, tsimikizirani kuti
 - a) azimayi ndi opirira
 - b) azibambo ndi ankhanza
 - c) akuluakulu amayendetsa zinthu/nkhani bwino
 - d) atengambali ena anali amantha
 - e) azimayi ndi achikondi
2. Kodi chisudzo cha *Mchira wa buluzi* ndi *Zikani* zikufanana bwanji?
3. Fotokozani zomwe mlembi akufuna kutiiza pa atengambali aamuna malingana ndi chisudzo cha *Khoswe wapadenga*.
4. Fotokozani zochitika zomwe zikutsimikizira kuti mlembi adagwiritsa ntchito msemphano m'zisudzo izi:
 - a) *Chamdothe*
 - b) *Khoswe wapadenga*
 - c) *Zikani*
5. Fotokozani kufunika kwa zivumbulutso zomwe zikupezeka m'chisudzo cha *Mchira wa buluzi*.
6. Ndi zinthu ziti zomwe zikusonyeza kuti zinthu sizimayenda bwino m'mudzi mwa Mfumu Tandwe ngakhale munali dongosolo?
7. "Azimayi adazunzika kamba ka amuna awo." Tsimikizani mawu amenewa ndi zochitika m'bukhu la *Chamdothe* ndi zisudzo zina.
8. "Munthu amakolola zomwe adafesa." Tsimikizirani mawuwa ndi zomwe zikuchitika m'bukhu la *Chamdothe* ndi zisudzo zina.
9. "Pamene makolo ena amalangiza ana zabwino, ena amawauza zoipa." Tsimikizirani mawuwa ndi zochitika m'bukhu la *Chamdothe* ndi zisudzo zina.